


KUKHAZIKITSIDWA ²

 Ine...ndachedwa pang'ono chabe. Ine ndinali ndi winawake wachiwawa, wachiwawa kwambiri, ndipo ine ndimayenera basi kuti ndipite pa nthawi imeneyo, chifukwa iwo anali moipa, kwambiri. Ndipo ayendetsa njira yonse kuchokera ku Michigan, wapolisi anaimba, ndi zina zotero, kuti iwo anali moipa, kwambiri. Tsopano, koma zikhala bwino; chirichonse—chirichonse chiri pansu pa ulamuliro, chotero ziri bwino. Pamene Ambuye abwera, chirichonse chimakhala pansu pa ulamuliro ndiye, sichoncho izo? Oh, Iye—Iye ndi wabwino kwambiri; kuganiza za ubwino Wake ndi chifundo Chake, za chimene Iye amatanthauza kwa ife, ndi mmene matamando Ake aliri ofunikira.

Chabwino, ife tinayesera kuyamba, kunena kuti ife titenga mitu yoyambirira itatu ya Bukhu la Aefeso. Ndipo ine ndikuganiza ife tinapeza mawu oyambirira atatu, kapena zoyambirira zitatu *zinazake* pamenepo. Ife sitinapite patali kwambiri, koma mwinamwake usikuuno ife tikhoza kupitirira patsogolo pang'ono. Tsopano, ine ndikufuna kunena kuti ine si wophunzira Baibulo, kutali tali, ndipo ndiri kutali kwambiri kuti ndingakhale wa fioloje, koma ine—ine ndimawakonda Ambuye, ndipo ine ndimakonda kumutumikira Iye ndi... [M'bale akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi].

Winawake, basi chadzidzidzi, akuti, basi ife tisanapitirire tsopano, mtsikana wamng'ono ali mchipatala mu Louisville, ndipo akatswiri apamwamba onse amukanika iye, iye akufa tsopano, ndipo akufunsa zopempha pa mwana yu. Ngati Akhristu, ndi ntchito yathu kuti tiweramitse mitu yathu, tsopano, ku pemphero.

Ambuye wathu wachisomo, si ntchito yathu kokha, koma ndi mwayi wathu, ndipo ndi chathu—chokhumba chathu kuti ife tiweramitse mitu yathu usikuuno ngati mpingo, ngati gulu la oitanidwa atuluke, anthu okhulupirira pano usikuuno, kuti tidzaphunzitse Mawu Anu, kutiika ife pamalo athu mu Thupi, pamene ife tikuyenera kukhalapo, ndi pamene ife tingakagwire ntchito moyenera pamodzi ngati ziwalo za Thupi la Khristu.

² Ndipo tsopano zafunsidwa pa ife kuti tipite mwamsanga kwa Mulungu. Ndipo aliyense wa ife abambo timaganiza kuti, nanga bwanji ameneyo akanakhala mtsikana wathu wamng'ono, momwe mitima yathu ikanatenthera ndi kupwetekedwa mkati mwathu, ndipo ife tikanaimbira matchalitchi kuti nthawi yomweyo akhale ndi pemphero. Ndipo mtima wa bambo wina ukutentha, ukupweteka. Ambuye, mulole Munthu wamkulu uja wa Mzimu Woyera abwere pakali pano ku mtima wa bambo

ameneyo. Muchotsepo mthunzi uliwonse wa kukaikira, ndi kupweteka kulikonse, ndipo mulole iye adziwe kuti Inu ndi Mulungu ndipo palibe nthenda imene ingaime mu Kukhalapo Kwanu pamene kutuma Kwanu kwa Umulungu kwachitika ndi mpingo Wanu ndi anthu Anu.

³ Ndipo monga kudutsa mu sabatayi, ife takhala tikupemphera, kuyambira Lamlungu lapitali ine ndimaganzira pa njira izi kapena kachitidwe aka ka pemphero. Ife tiribe zida zochulukira monga mwa kawonedwe ka dziko, koma legeni yaing'ono iyi ndi yakupha pamene iyo igwiridwa ndi zala za chikhulupiriro. O Ambuye, mulole mapemphero athu akafike mkati, kuti imfa imeneyo uko imene yapachikika pa mwana ameneyo, ndipo mulole iyo isweke; mdima, kulunda, zichoke pambali ya bedi ya khanda limenelo, khanda kapena mwana ameneyo, mtsikana wamng'ono. Ndipo mulole Kuwala kwakukuru kwa Kukhalapo kwa Mulungu kuwalire pa iye. Mulole iye atuluke ku chipatala chimenecho, ali mwana wabwino bwino.

⁴ Mulungu, ife tikudziwa kuti kungwoloka mtsinje okonedwa athu akudikirira, ndipo izo ndi za ulemelero. Koma ife timawakonda achichepere athu. Ndipo ife tikupemphera, Ambuye, chifukwa cha ulemelero Wanu, kuti Inu muwupulumutse moyo wa mwana ameneyo. Ife, ngati mpingo Wanu, tikuidzudzula imfa imeneyo, ndipo tikuti, “Ima nji kumeneko. Iwe sungamutenge mwana ameneyo, chifukwa ife tikuwuitanitsa moyo wake pa chifukwa cha ufumu wa Mulungu.” Perekani zinthu izi, Ambuye, kuti zipite molunjika pa chandamale pamene ife tikuzilunjikitsa izo, mu Dzina la Yesu Khristu, Mpulumutsi wathu. Amen.

⁵ Kodi ife tikukhulupirira? Ine sindikudziwa chimene ine ndikanachita ngati ine ndikanati ndisakhale Mkhristu. Ine basi sindikanafuna kukhala nthawi yaitali. Palibepo chirichonse chokhalira moyo, basi kuti ndiziwatengera ena kuti apulumutsidwe, ndicho chopambana chimene ine ndimachidziwa.

⁶ Tsopano, usikuuno ife tikufuna tingoyamba maziko pang'ono a phunziro lathu la mmbuyo. Ndipo ine ndiyetsa kuti ndiwerenge, chifukwa, mutu wonsewo, ngati ine ndingathe usikuuno. Chotero Lamlungu mmawa ine ndidzayenera mwinamwake kukankhiramo ziwiri zonse Lamlungu mmawa ndi usiku, ngati izo ziri zabwino, kudzayetsa kudzalowa mu kachitidwe aka kamene ine ndikufuna kuti mpingo ukawone. Oh, izo ndi zaulemelero kupeza malo ako! Ndipo palibe amene angachite chirichonse pokhapokha iwe utadziwa bwino bwino chimene iwe ukuchita.

⁷ Nanga bwanji ngati inu mukanati mukukakhala... mukukakhala ndi opareshoni, ndipo nkukhala kuti kuli dokotala

wachichepere amene wangobwera kumene kuchokera ku sukulu kuti iye akufuna. . . sanayambe wapangapo opareshoni mmbuyomo. Komabe, iye ndi wamng'ono ndi wowoneka bwino, ndipo tsitsi lake lapededwa monyolola, ndipo iye wavala bwino, akuwoneka bwino, ndi chirichonse. Ndipo iye akuti, "Ine ndanola mipeni, ndipo ndatenthetsa zipangizo zonse ndi zinthu." Koma inu mukhoza kukhala ndi kumverera kwachirendo pang'ono ndi zimenezo. Ine kulibwino ndikhale ndi dokotala wokalamba amene anachitapo opareshoni imeneyo nthawi zambiri mbiri mmbuyomo, ine ndisanafune kuti ndidulidwe. Ine—ine ndingafune kudziwa winawake osati wongochokera kumene ku sukulu, ine ndingafune winawake woti anachitapo zimenezo.

⁸ Ndipo Mmodzi wodziwa bwino ntchito amene ine ndikumudziwa, woti ndimuitane usikuuno, ndi Mzimu Woyera. Iyeyo ndi Msing'anga wamkulu wa Mulungu ndi Mphunzitsi wamkulu.

⁹ Ndipo ngati maziko a Uthenga wanga usikuuno, kuchokerabe ku uthenga wa Lamlungu, kuti iwo ndi. . . Iwo anamukana Samuele ndi Mawu a Ambuye; ndipo iwo anamuvomereza Saulo, mwana wa Kishi; ndipo anamukana Samuele, yemwe ankaimira Mzimu Woyera, chifukwa iye ankangoyankhula monga Mzimu umamutsogolera iye kuti ayankhule. Ndipo pamene iye anaitanira tcheru chawo kwa izo, iye anati, "Kumbukirani, ine sindinayambe ndayankhulapo kanthu kwa inu mu Dzina la Ambuye koma chimene Ambuye anachikwaniritsa. Komanso ine sindinayendepo mopanda khalidwe pamaso panu. Ndipo palibe mmodzi yemwe anganditsutse ine za tchimo."

Monga Yesu anati, "Ndani anganditsutse Ine za tchimo?" Mukuona?

¹⁰ Ndipo ananenanso, kuti, "Ine sindinabwere kwa inu ndi kudzakupemphani inu ndalama ndi zina zotero. Ine sindinatenge kalikonse kwa inu. Koma zonse zimene ine ndazinena zakhala ziri kwa ubwino wanu, zimenezo ine ndimazibweretsa kwa inu kuchokera pa kamwa ya Ambuye."

¹¹ Ndipo anthu onsewo anaperekera umboni, "Izo nzoona. Zonsezo ndi zoonza, komabe ife tikufuna kukhala ndi mfumu. Ife tikufuna kuti tikhale monga dziko lonse."

¹² Tsopano, usikuuno, Lemba lathu likugawaniza Bukhu la Aefeso, ndi Bukhu la Yoswa la Chipangano Chatsopano. Ilo likugawaniza ndipo likuyika mu dongosolo "ogonjetsawo." Tsopano, amenewo ndi maziko chabe kwa maminiti pang'ono, kuti tipeze malo ife tisanayambe kuwerenga, kuyambira ndi ndime ya 3. Tsopano, ife tinapeza Lamlungu lapitali usiku kuti. . . Mulungu mu Chipangano Chakale anamupangira Israeli lonjezo la dziko la mpumulo, chifukwa iwo anali

atasanduka amwendamnjira ndi oyendayenda. Ndipo iwo anali mdziko limene silinali lawo, ndipo Mulungu anali atalonjeza kudzera mwa Abrahamu kuti iye adzakayenda, mbewu yake ikanadzakayenda kwa zaka foro handiredi kwa anthu achirendo, ndipo adzakazunzidwa, koma ndi dzanja lamphamvu Iye akanadzawaturutsako iwo kuti akalowe mdziko labwino limene linali loyenda mkaka ndi uchi.

¹³ Ndipo, tsopano, pamene nthawi ya lonjezo inkayandikira pafupi, Mulungu anamudzutsa winawake woti awabweretse iwo ku dziko limenelo. Ndi angati m'kalasi usikuuno kuti ameneyo anali ndani... akudziwa kuti ameneyo anali ndani? Mose. Zindikirani, chenicheni, choimira chenicheni cha Mmodzi wathu amene anaperekedwa kuti atibweretse ife kupita ku Dziko lolonjezedwa, Khristu. Tsopano ife tiri ndi lonjezo, chifukwa lonjezo lathu ndi Mpumulo wauzimu, pamene, wawo unali mpumulo wathupi. Ndipo chotero iwo anali kubwera ku dziko limene iwo akanadzakhoza kumati, "Ili ndi dziko lathu, ife sitirinso amwendamnjira ife takhazikika, ili ndi dziko lathu, ndipo kuno ife tiri ndi mpumulo. Ife tibzala chimanga chathu, minda yathu ya mpesa, ndipo ife tizidya kuchokera mminda yathu ya mpesa. Ndiyeno tikadzafa, ife tidzasiyira iyo kwa ana athu."

¹⁴ Oh, mmene ife tingakalowera mdziko limenelo, malamulo a cholowa, monga Naomi ndi Rute, Boazi. Kuzibwezeretsanso zonsezo. Momwe m'bale mu Israeli, momwe iye akuyenera... chirichonse chimene iye anachitaya chikuyenera kuwomboledwa ndi wachibale. Oh, ndi zokongola bwanji! Izo zikhoza kutenga masabata ndi masabata ndi masabata ndi masabata, osakhoza kuchoka pa mutu uwu, kuti tipite kwa izo. Ife tikhoza kumangiriza Baibulo lonselo pomwe apa mu izi, pa mutu umodzi uwu kumene.

¹⁵ Ndipo, oh, ine ndimangokonda kuwerenga Ilo. Ife tinkakonda kulitenga Ilo, ndi kutenga izo kwa chaka ndi theka, ndipo osachokako nkomwe ku Bukhulo. Kungokhala pomwepo ndi Ilo.

¹⁶ Tsopano, koma, icho chinali chinthu chachikulu chotero chimene cholowacho, mmene zinkakhallira kuti cholowa mdziko kuti sipamakhala wina aliyense koma wachibale wapafupi ndi amene amatha kuwombola cholowa chimenecho. Tsopano, mundilole ine ndingogwetsera chizindikiro pang'ono apa chimene ine ndinachikhudza usiku wina, kwa inu amayi. Ndi angati pano amene munawapemphererapo okonedwa anu, odayika? Chabwino. Ndi zimenezotu aponso, mwaona, "Cholowa chanu." Mukuona?

¹⁷ Paulo anamuuzwa wa Chiroma, anati, "Ukhulupirire pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo iwe ndi nyumba yako mudzapulumutsidwa." Ngati iwe uli ndi chikhulupiriro

chokwanira cha iwemwini kuti upulumutsidwe, ukhale ndi chikhulupiriro chokwanira, ziribe kanthu kuti mnyamata ameneyo wasochera chotani, kapena mtsikana ameneyo, iwo adzapulumutsidwabe mulimonse. Mulungu, mwanjiraina! Kaya Iye adzachita kukawagoneka iwo pansana wawo, kukagona uko mchipatala, akufa, iwo adzapulumutsidwa. Mulungu analonjeza zimenezo. Cholowa! Oh! “Ndipo iwo adzakakhala kumeneko,” anatero Yesaya, “ndipo mphukira zawo zonse limodzi ndi iwo. Iwo sadzavulazidwa kapena kuwonongedwa mu phiri Langa lonse loyera, atero Ambuye.”

¹⁸ Oh, ine ndiri ndi kamalo kakang’ono kamene ine ndikudalira kuti ndikhoza kufikapo usikuuno, chifukwa cha inu. Zikungotentha mu mtima mwanga, kuti ndibwererenso kwa izo.

¹⁹ Koma tsopano, tipite patsogolo. Ndiye kodi inu munamuzindikira Mose, wochita zozizwitsa wopambana uja amene anamubweretsa Israeli mpaka kudutsa mdzikolo, ndipo anawafikitsa iwo mpaka ku dziko lolonjezedwa, koma sanaike cholandira chawo kwa iwo? Iye sanawapatse iwo cholandira chawo; iye anawatsogolera iwo mpaka ku dzikolo, koma Yoswa anadzagawaniza dzikolo kwa anthu. Nkulondola uko? Ndipo Khristu anawubweretsa mpingo kudzafika pa malo amene cholowa chawo chinadzapangidwa kwa iwo, chinadzaperekedwa kwa iwo, atangotsala ndi Yordani kuti amuwoloke, koma Mzimu Woyera ndi Iwowo Umene ukuyika mpingo mu dongosolo. Yoswa wa lero akuwuika mpingo mu dongosolo lake, akupereka kwa mmodzi aliyense, mphatso, malo, udindo. Ndipo Iye ndi Liwu la Mulungu likuyankhula kudzera mwa munthu wamkati amene Khristu wamupulumutsa, Mzimu Woyera. Tsopano kodi inu mukumvetsa bwino zochuluka za izo? Tsopano ife tikufika mu Bukhu la Aefeso. Tsopano, mwanjira yomweyo, Iye akuwuyika mpingo pamalo pamene iwo ukuyenera kukhalapo. Tsopano, Yoswa anawayika iwo mu dziko la chirengedwe. Lero Mzimu Woyera ukuwuyika mpingo, pamalo ake, mu dziko, limene iwo, pa malo amene iwo akuyenera kukhalapo, cholowa chawo.

²⁰ Tsopano, chinthu choyamba chimene iye akuyambira apa, iye akulemba kalata yake, “Paulo.” Zimene, ife tizipeza pakapita kanthawi kuti chinsinsi chonse ichi chinaululidwa kwa iye, osati mu seminare, osati ndi wa fioloje aliyense, koma ilo linali vumbulutso Laumulungu la Mzimu Woyera limene Mulungu anamupatsa Paulo. Podziwa kuti chinsinsi cha Mulungu, iye anati, chimene chinali chitabisidwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, chinali chitaululidwa kwa iye mwa Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu Woyera pakati pa anthu unali kumuyika aliyense mu dongosolo, kuwuyika mpingo mmalo.

²¹ Tsopano, chinthu choyamba chimene Paulo akuyamba nacho apa kuwauza anthu, ndi kuwatenga onse...Kumbukirani, izi

ndi za kwa mpingo, osati kwa wakunja. Icho ndi chinsinsi mmafanizo kwa iye, samatha konse kuti amvetse, zimapita pamwamba pa mutu wake, iye samadziwa konse za icho kuposa kalikonse. Koma, kwa mpingo, icho ndi uchi mu thanthwe, icho ndi chimwemwe chosaneneka, icho ndi chitsimikizo chodala, icho ndi nangula ya solo, icho ndi chiyembekezo chatu ndi pokhalapo, icho ndi Thanthe la Mibadwo, oh, icho ndi chirichonse chimene chiri chabwino. Pakuti miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu a Mulungu sadzapita.

²² Koma munthu wakunja kwa Kenani samadziwa kalikonse za zimenezo, iye akuyenda yendabe. Sindikunena kuti iyeyo si munthu wabwino, ine sindikunena zimenezo. Ine sindikunena kuti munthu ngakhale wa mu Igupto si munthu wabwino, koma iye, kufikira iye atabwera ku cholowa ichi.

²³ Ndipo cholowacho, chimene, lonjezo limene linaperekedwa kwa mpingo si dziko la chirengedwe, koma dziko lauzimu, pakuti ife ndi unsembe wachifumu, fuko loyera. Ndiye mu unsembe wachifumu uwu, fuko loyera, anthu achirendo, oitanidwa atuluke, osankhidwa, osankhulidwa, oyikidwa pambali, ndiye dziko lonse limakhala lakufa kunjaku. Ndipo ife timatsogozedwa ndi Mzimu. Ana aamuna ndi aakazi a Mulungu amatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu; osati ndi munthu, koma ndi Mzimu.

²⁴ Onse mu chikondi, chinthu chonsecho chimamangidwa mu mtolo tsopano. Ichi chayesedwapo kuphunzitsidwa nthawi zambiri, ndipo sindikukaika kuti afioloje aakulu achikhudzapo icho mwakuya kwambiri kuposa mmene ine ndingachitire. Koma chinthu chimene ine ndikufuna kuti ndiyesere kuchipereka kwa inu ndi ichi, kuti munthu yemwe ali mwa Khristu, wokhala ndi Mzimu Woyera, akhoza kupirira naye munthu pamene iye akulakwitsa, amakhala woleza mtima, wofatsa, wopirira. Iye amakhala wokoma, wodzichepetsa, wokhulupirika, wodzazidwa ndi Mzimu, samakhala woipidwa, nthawizonse amakhala wokoma. Iye amakhala munthu wosinthika.

²⁵ Osati kungokhala munthu wakuti, “Ife nthawiina tinali nazo izo. Ngati ife tinafuula, ife tinalandila izo, ife a Methodisti. Oh, pamene ife tinafuula, ife tinali mu Dzikolo.” Zimenezo ndi zabwino, zimenezo nzovomerezeka, ine ndimakhulupirira zimenezo nanenso.

²⁶ Kenako potsatira a Pentekoste anadzabwera akuyankhula ndi malirime, iwo, “Anali nazo; aliyense amene anayankhula ndi malirime anali nazo izo.” Ine ndikukhulupirira zimenezo, nanenso. Komabe ife tinadzapeza kuti ambiri sanalandire Iwo apobe, inu mwaona. Mukuona? Tsopano iwo ali . . .

²⁷ Tsopano ife tikubwera ku chinsinsi chobisika chachikulu ichi chimene chakhala chobisidwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi ndipo tsopano chikuululidwa mmasiku otsiriza

kwa ana aamuna a Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo kukhala zoonza, kuti ana a Mulungu akuwonetseredwa? Ife tisanapite nkomwe kulikonse, tiyeni titsegule ku Aroma mutu wa 8 miniti chabe, mundilole ine ndiwerenge kwa inu chinachake. Tiwone ngati ichi chikubwera kwa chimene ine ndikuchikamba apa. Tsopano ife tipeza Aroma 8, ndime ya 19 ya—ya mutu wa 8 wa Aroma.

Pakuti chiyembekezo choonamtima...chirengedwe chikudikirira kuwonetseredwa kwa ana a Mulungu.

²⁸ Ndi chiyembekezo choonamtima, chirengedwe chonse chikudikirira kuwonetseredwa. Mwaona, kuwonetseredwa! Kodi kuwonetseredwa ndi chiyani? Kuchipanga kuti chidziwike!

²⁹ Dziko lonse. Achimuhamedi kutsidya uko, iwo akuyembekeza zimenezo. Kuzungulira konse, kulikonseko, iwo akuyembekeza zimenezo. “Ali kuti anthu amenewa?” Ife takhalapo nazo a...Ife takhalapo nayo mphepo ya nkokomo wamphamvu, ife takhalapo nawo mabingu ndi mphenzi, ife takhalapo nawo mafuta ndi magari, ife takhalapo nayo mitundu yonse ya zinthu; koma ife tinalephera kumvetsera Liwu laling’ono lakayeziyezi lija limene linamukopa mneneri, amene anavala mwinjiro ndipo nachokapo, ndikuti, “Ndine pano, Ambuye.” Mukuona?

³⁰ Tsopano chirengedwe chonse chikubuula ndi kudikirira kuwonetseredwa kwa ana aamuna a Mulungu. Tsopano, Paulo poyamba akupita kukawuyika mpingo ndendende kumene iwo ukuyenera kukhala. Tsopano kuti tingopeza maziko, tiyeni tiwerenge kenanso.

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, kwa oyera (amenewo ndi “oyeretsedwawo”) amene ali ku Efeso, ndi...okhulupirika mwa Khristu Yesu:

³¹ Tsopano, kuti kalasi isaiwale izi, kodi timalowa chotani mwa Khristu? Kodi ife timajowina mpingo kuti tilowe mwa Khristu? Kodi ife timapanga kudzinenera kuti tilowe mwa Khristu? Kodi ife timamizidwa mmadzi kuti tilowe mwa Khristu? Ife timalowa chotani mwa Khristu? Akorinto Woyamba, mutu wa 12, “Pakuti ndi Mzimu umodzi,” umodzi, chirembo chachikulu M-z-i-m-u, umene uli Mzimu Woyera, “ife tonse timabatizidwa kulowa mu Dziko lolonjzedwa.”

³² Mu Dziko lolonjzedwa ili, chirichonse ndi chatu mu Dziko lolonjzedwa. Mukuona zimenezo, M’bale Collins? Mwaona, chirichonse mu dziko lolonjzedwa! Pamene Israeli anawoloka Yordani uyu, kukalowa mu Dziko lolonjzedwa, anamenyera chirichonse!

³³ Tsopano kumbukirani, mu Dziko lolonjzedwa ili, zimenezo sizikutanthauza kuti ndinu otetezeka ku matenda, zimenezo

sizikutanthauza kuti ndinu otetezeka ku mavuto. Koma izo zimakamba izi, (oh, mulole izi zizame mwakuya), izo zimanena izi, kuti ilo ndi lanu! Mungodzuka ndi kukalitenga ilo! Mukuona? Pamene. . .

³⁴ Ndipo, kumbukirani, njira yokhayo imene Israeli amataira munthu, ndi pamene tchimo lilowa mu msasa. Ndiyo njira yokhayo imene ife tingataire konse a—chigonjetso, ndi kuti tchimo lilowe mu msasa, chinachake chitalakwika penapake. Pamene Akani anaba chikute chija ndi chovala cha wa Chibabulo uja, tchimo linadzabwera mu msasa, ndipo nkondo inadzavuta.

³⁵ Inu mundipatse ine uwu—mpingo uwu usikuuno, gulu ili la anthu, mwangwiro, mwangwiro mu lonjezo la Mulungu, ndi Mzimu Woyera, kumayenda mu Mzimu, ine ndikutsutsa nthenda iliyonse kapena chosautsa chirichonse, kapena chirichonse chimene chiripo, Joe Lewis aliyense amene alipo mu dziko, ndi chikunja chake chonse, ndi osakhulupirira onse amene alipo, kuti abweretse nthenda iliyonse kapena chosautsa pa khomo ili, ndipo iwo azichoka pano atachira mwangwiro. Inde, bwana. Mulungu anapereka lonjezo, tchimo lokha la kusakhulupirira ndi limene likhoza kuthamangitsa izo. Tsopano ife titsikira mmusi ku chimene tchimo laling'ono ili liri, pakapita kanthawi, tsopano.

. . . amene tiri *mwa Khristu Yesu:*

Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, zochokera kwa Mulungu Atate wathu, ndi. . . Ambuye Yesu Khristu.

Odala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye Yesu Khristu athu, amene watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mmalo ammwambamwamba mwa Khristu, mwa—mwa Khristu:

³⁶ Pamene ife tikhala mwa Khristu, ife timakhala ndi mdalitso wauzimu. Kunja kwa Khristu, ife timakhala ndi zogirigisha. Mwa Khristu ife timakhala ndi mdalitso weniweni. Osati zodzipangitsa-kukhulupirira, osati zonyengezera, osati zongovala. Koma nthawizonse pamene inu mukumayesera kunena kuti inu muli mu Dziko lolonjezedwa, ndipo simuli, machimo anu adzakakupezani inu. Ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, inu mudzazipeza nokha wachinyengo ndi—ndipo zonse, monga momwe ife timazitchulira izo mdziko, odetsedwa. Inu mudzapeza kuti mulibe zimene inu mukuzikambazo. Koma pamene inu mukhala mwa Khristu Yesu, Iye anakulonjezani inu mtendere wa Mmwambamwamba, madalitso a Mmwambamwamba, Mzimu wa Mmwambamwamba, chirichonse ndi chanu. Inu muli mu Dziko lolonjezedwa ndipo mwatenga kwathunthu chirichonse. Ameni. Ndi zokongola bwanji! Oh, tiyeni tiwerenge.

Monga momwe iye watisankhira ife . . .

³⁷ Tsopano, apa ndi pamene mpingo umapunthwa moipa kwambiri.

Monga momwe iye anatisankhira ife mwa iye . . . (Mwa Ndani?) Khristu.

³⁸ Ife tikupeza tsopano, mmbuyo mu—mu Genesis ndi mu Chivumbulutso, Chivumbulutso 17:8, kuti Iye anatisankha ife mwa Khristu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Tsopano, mawu . . . Ndiloleni ndiwerenge yotsatirayo.

. . . maziko a dziko lapansi, kuti ife tikakhale oyera ndi opanda chilema pamaso pa iye . . .

Atatikonzeratu ife . . .

³⁹ Tsopano ine ndikufuna ndiimire pa liwu limenero la “kukonzedweratu.” Tsopano, *kukonzedweratu* si kunena kuti, “Ine ndimusankha M’bale Neville, ndipo ine—ine—ine—ine—ine sindimusankha M’bale Beeler.” Zimenezo sindizo ayi. Izo ndi kudziwidwiratu kwa Mulungu kumene kunadziwa kuti ndi uti adzakhale wabwino ndi amene sadzakhala wabwino. Chotero, mwakudziwidwiratu, Mulungu podziwa chimene Iye akanati adzachite, Iye anakonzeratu mwa kudziwiratu Kwake kuti akapange zinthu zonse zikagwire ntchito kwa ubwino wa iwo amene amamukonda Mulungu, kuti Iye adzakhoze, mu m’badwo umene uli nkudza, kuitanira zinthu zonse mwa Mmodzi, amene ali Khristu Yesu.

⁴⁰ Mundilole ine ndikujambulireni inu chofotokoza chaching’ono apa. Icho ndi chabwino. Ife tibwerere mmbuyo, ine ndikukhulupirira ndinayankhula pa izo pang’ono usiku wina, kapena ndinakhudzapo izo, mu Genesis, mutu wa 1, 1:26, pamene Mulungu anadzitchula Dzina Lake, “Ambuye Mulungu,” izo ziri mu liwu la El, Elah, Elohim, zimene zimatanthauza “Uyo wokhalapo-yekhayo.” Panalibe chirichonse chimene chimakhalapo koma Iye. Kunalibe mpweya, kunalibe kuwala, kunalibe nyenyezi, kunalibe dziko, kunalibe china chirichonse. Anangokhala Mulungu, ndipo Mulungu yekha, El, Elah, Elohim. Tsopano, Iye anapanga zimenezo.

⁴¹ Mkati mwa zimenezo munali zikhumbo zimene zimatanthauza kuti Iye anali . . . Mkati mwa El, Elah, Elohim wamkulu uyu munali chikhumbo kapena . . . Inu mukudziwa chimene *chikhumbo* chiri, kapena ndiloleni ine ndinene zimenezo monga chonchi, chinali “chikhaliidwe.” Kuchitira kuti ana amvetse izo, ndipo ndine mmodzi wa anawo amene akuyenera kumvetisa izo mwanjira imeneyo. Mkati mwa Iye munali chikhaliidwe choti adzakhale atate, koma Iye ndi wokhalapo-yekha, panalibepo chirichonse choti Iye akhalire Atate. Ndipo, tsopano, mmusi mkati mwa izo munali chinachakenso, kuti Iye anali Mulungu; ndipo mulungu ndi chinthu chopembedzedwa; koma Iye anali wokhalapo-

yekha, El, Elah, Elah, Elohim, chotero panalibe chinthu choti chizimupembedza Iye. Mkati mwa zimenezo, Iye anali Mpulumutsi, ndipo panalibe chirichonse chimene chinataika choti chipulumutsidwe. Mukuona? Mkati mwa zimenezo, Iye anali Mchiritsi, mwaona, koma panalibe chirichonse chimene chimadwala choti chichiritsidwe, kapena chirichonse choti chidwale. Tsopano kodi inu mukuchimvetsa chithunzicho? Chotero zikhumbo Zake, chikhaliidwe Chake chinabala chimene chiripo lero.

⁴² Anthu ena amati, “Chabwino, nchifukwa chiyani Mulungu sanangozimitsa izo pachiyambi?” “Iye ndi mthakati wa mtima wankhanza,” anatero Joe Lewis, iye amene anamuweruza Joe, kapena Jack Coe, mwaona. Anati, “Iye ndi mthakati basi wa mtima wankhanza. Palibepo chinthu chotero ngati Mulungu. Ngati pakanakhala kuti chinalipo chinthu choterocho, Iye akanakhala a...” Oh, ine... anangomutchula Iye mitundu yonse ya maina, mwaona. Koma izo ndi chifukwa chakuti iye mwina anali ndi chidziwitso chambiri mmwamba *umu*, koma iye analibe kalikonse mmusi *umu*.

⁴³ Tsopano, zimenezo, apo ndi pamene izo ziri. Mukuona? Mawu awa akunena izo apa, ndipo Iye anzibisa izo. Ndipo zinsinsi izi zakhala zobisidwa tsopano, kumbukirani, Baibulo linati, “Chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, kudikirira kuwonetseredwa kwa ana a Mulungu,” kuti adzawonetsere izo kwa mpingo. Oh, mai! Inu mukumvetsa zimenezo?

⁴⁴ Tsopano ine ndiimikire pa nkhani yanga pang’ono chabe, kapena ine ndiibweretsa... Ine ndipita ku lingaliro langa lotsatira kuti ndipeze izi. Tsopano kumbukirani, kudutsa mmibadwo yonse ya Mose, kubwerera kudzadutsa mmibadwo ya aneneri, kubwerera kudzadutsa mibadwo yonse, iwo akhala akudikirira mpaka masiku otsiriza ano kuti zinthu izi zidzawonetseredwe, mogwirizana ndi Lemba. Uko nkulondola, kuti izo zidzaululidwe kwa ana a Mulungu. Chifukwa chiyani? Kuchokera kwa otayika... kudzafika pofanana ndi piramidi, monga ine ndanenera, amamanga moyandikira, yandikira, yandikira.

⁴⁵ Monga ine kawirikawiri ndakhala ndikunena ndemanga iyi, ndipo ndinati, Mulungu anapanga Mabaibulo atatu. Loyamba, Iye anadzaliyika Ilo mu mlengalenga, zodiaki. Kodi inu munayamba mwaiwonapo zodiaki? Chithunzi choyambirira mu zodiaki ndi chiyani? Namwali. Chithunzi chomalizira mu zodiaki ndi chiyani? Leo mkango. Iye anabwera nthawi yoyamba kwa namwali, Iye akubwera kachiwiri ngati Mkango wa fuko la Yuda. Mukuona?

⁴⁶ Iye anadzapanga lotsatira mu piramidi, kumbuyo mmasiku a Enoki, pamene iwo anapanga piramidi. Ndipo iwo amaziyeza izo. Ine sindimamvetsa izo. Koma kukafika ku nkondo,

kumene iwo ankawerama ndi kumakayenda pa mawondo awo kwa mtunda wautali, ndipo amakhoza kuyeza mtunda wa nkhondo. Inu mukudziwa kuti iwo amayeza mpaka kuti lero? Patsidya kudutsa chipinda cha mfumu. Ndipo pamene piramidi iyi inkakwera mmwamba...Ife sitingakhoze kuimanga iyo, ndi chirichonse chimene ife tiri nacho lero. Ife sitingakhoze kuimanga iyo.

⁴⁷ Iyo inamangidwa chokwera monga *chonchi*, mpaka pa nsonga. Ndipo mwala pa...Mwalawophimba supezeka nkome. Iwo samaika nkome chivinikiro pamwamba pa piramidiyo. Ine sindikudziwa ngati inu mukudziwa zimenezo kapena ayi, piramidi yaikulu yaku Igupto, iyo siimakhala konse ndi mwala wapamwamba pa iyo. Chifukwa chiyani? Mwalawophimba unakanidwa, Khristu, Mwalawapamutu, mwaona, unakanidwa.

⁴⁸ Koma pamene ife tikukula kuchokera ku m’badwo wa Lutera, m’badwo wa Baptisti, m’badwo wa Methodist, m’badwo wa Pentekoste, ife tafika penipenipo mpaka pa Mwala wophimba tsopano, mwaona, kudikirira ndi kuyembekezera kuti Mwala wophimbawo ukhazikidwe pansu, nyumbayo yatha. Kodi inu simunawerengapo mu Lemba, “Mwala unakanidwa”? Ndithudi, ife tikuzindikira kuti zimenezo amakamba za kachisi wa Solomoni. “Koma Mwala wokanidwawo wasanduka Mwini wa ngodya.” Ndipo ine ndikunena izi kuti ndingopanga a—a— a—a chithunzi kwa inu.

⁴⁹ Tsopano, ndipo mu Baibulo, ife tikukhala mu tsiku lotsiriza, pamwamba pa piramidi, nsomba zopingisana za m’badwo wa khansa mu zodiaki, mu nthawi ya kudza kwa Leo mkango, mu mwala wophimba, ndi mmasiku a kuwonetseredwa kwa ana a Mulungu, mu Baibulo, mwaona. Mukuona pamene ife tiri? Ife tiri penipenipo pamapeto a nthawi.

⁵⁰ Ndi angati amene akhala akuwerenga pepala sabata ino, zimene Khrushchev ndi iwo anena? Oh, iwo ndi okonzeka; nafenso tatero. Amen. Takonzeka! Izo ziri bwino, mwaona. Oh, ndi—ndi—ndi chamwayi bwanji, ndi tsiku bwanji! Ngati Akhristu akanangozindikira tsiku limene ife tikukhalamo. Mai!

⁵¹ Kodi inu mukuganiza chiyani? Wolemba wa Bukhu ili, amene anaziwona izo, ndipo anawona kumene izo zikanadzawonetseredwa mmasiku otsiriza, akudikirira ndipo akubuulira ana amenewo a Mulungu kuti awuke mmasiku otsiriza, ndi mphamvu ya Mzimu Woyera kumapeto a m’badwo, kuti adzawulule zinthu zachinsinsi kuyambira ku maziko a dziko lapansi, ndi kuzibweretsa izo poyera.

⁵² Tsopano tiyeni tibwerere tikalowe ku “maziko a dziko lapansi” kenanso, kuti tikapeze vumbulutso, kuti tikawone ngati ife tikulondola kapena ayi. Ine ndikuyembekeza kuti sindikuzisinjirira ndekha pomutchula Mulungu, “Papa,” koma

ine ndikufuna kuti ndinene izi mwanjira imeneyo kuti inu mumvetse izo. Papa! Papa ankafuna ana ena, chotero kodi Iye anachita chiyani? Iye anati, “Pakhale Angelo.” Ndipo Iwo anabwera kudzamuzungulira Iye. Oh, izo zinali zabwino. Iwo ankampembedza Iye, zitatero Iye anadzakhala Mulungu, zikhumbo. Kumbukirani, Iye anali El (E-l), Elah, Elohim, wokhalapo-yekha, kunalibe chirichonse koma Iye. Chinthu choyamba chimene chinadzabwera chinali Angelo. Kenako, Angelo samachita china kuposa kupembedza. Iwo sakanakhoza kutaika. Chotero, Iwo sakanakhoza kudwala, Iwo anali zinthu zachisavundi. Chotero, Iye sakanakhoza kuwonetsera mphamvu Yake yochiritsa, Iye sakanakhoza kuwonetsera chipulumutso Chake. Chotero zitatero, mmbuyo, tsopano mulole. . .

⁵³ Ndiye zitachitika zimenezo, Iye anati, “Ife tipanga chinachake chogwirika.” Chotero Iye anapanga dziko lapansi. Ndipo pamene Iye anadzapanga dziko lapansi, Iye anapanga zolengedwa zonse za pa dziko lapansi, ndipo atatero Iye anamupanga munthu. Chirichonse chimene chinkatulukirapo kuchokera mnthaka; kuyambira ndi a—mbululu kapena nsomba yopanda minga, kungokhala maonekedwe chabe a mnofu ukuyandama pa madzi, zinayambira kuchokera pamenepo, mpaka. . . kuchokera pamenepo kudzakhala chule, umene ndi mtundu wa moyo wotsikitsitsa umene ife tingathe kuwupeza, iwo amatero, ndi chule. Mtundu wapamwamba ndi munthu. Kuchokera kwa chule izo zinayambira kwa buluzi, zitachoka kwa buluzi zimapita ndi kumapita ndi kumapita, ndipo nthawi iliyonse Mzimu Woyera ukayamba kuchita “whuushi,” kupuma, moyo unkabwera kenanso; “whuuushi,” moyo wokulirapo. Ndipo chinthu choyambirira, chinachake chinadzabwera mchifaniziro cha Mulungu, ameneyo anali munthu. Sipanayambe pakhalapo chirichonse, sipanayambe pakhalapo, sichidzalengedwa nkomwe chirichonse, chirichonse chapamwamba kumuposa munthu, chifukwa munthu ali mu chifanizo cha Mulungu. Mukuona?

⁵⁴ Ndiye munthu, pamene Iye anampanga munthu Wake woyamba. Tsopano, pamene Iye anapanga zolengedwa Zake za Ungelo. . . Iye anampanga munthu, “Iye anawalenga iwo mwamuna ndi mkazi,” onse mu thunthu limodzi. Iye anali ziwiri zonse mwamuna ndi mkazi, chachikazi ndi chachimuna. Pamene Iye anamupanga Adamu ndi kudzamuika iye mu mnofu. . . kumbukirani mu Genesis 1, Iye anapanga mwamuna ndi mkazi. Ndipo mu Genesis 2, panali palibe apabe munthu woti azilima mnthaka, munthu wa mnofu. Panalibe munthu yemwe akanamadzagwira chirichonse ndi kulima mnthaka, komabe panali munthu mu chifanizo Chake. “Ndipo Mulungu ndi. . .” [Osonkhana akuti, “Mzimu”—Mkonzi]. Uko nkulondola. Mukuona? Iye anampanga munthu woyamba, “mwamuna ndi

mkazi Iye anawalenga iwo.” Tsopano, pamene Iye anamupanga munthu woyamba!

⁵⁵ Tsopano, kumbukirani, zonse pamodzi Iye anali nazo izo mmalingaliro Ake. Ndipo Lamlungu usiku ine ndinadutsa zimenezo. A—liwu ndi lingaliro lofotokozedwa. Mulungu anaganiza mmene Iye akanadzakhalira Mulungu, mmene Iye akanadzamapembedzedwera, mmene Iye akanadzakhalira Mchiritsi, mmene Iye akanadzakhalira Mpulumutsi; ndipo mwamsanga pamene Iye anayankhula Mawu, izo zinatsirizika kwanthawizonse. Oh, ngati ana awa a Mulungu tsopano angagwire Mawu amenewo monga chomwecho. Pamene Mulungu ayankhula Mawu, izo zimakhala kuti zatha! Mwamtheradi! Iye mwinamwake anadikirira... Mndandanda wa mibadwo umanena zimenezo, kapena ofukula zamakedzana ndi onse, iwo amanena kuti mwinamwake dziko linali mamilioni ndi mamilioni ndi milioni. Ine sindikudziwa, ilo mwinamwake linali matrilioni ndi matrilioni a zaka. Ine sindikudziwa kuti izo zinatenga nthawi yaitali bwanji. Mulungu samakhala mu nthawi. Iye alibe nthawi yotsikira ndi miniti imodzi kuposa imene Iye anali nayo pa nthawi imene Iye ankayankhula izo. Iye akadali Mulungu panobe. Iye samakhala ndi nthawi.

⁵⁶ Ine sindinkazidziwa nkomwe izo monga chomwecho mpaka usiku wina, mmawa wina, kani. Wamuyaya, alibe dzulo, alibe mawa, izo zonse zimakhala za lero. Kodi inu munayamba mwazindikirapo mawu akuti “INE NDINE”? Osati “Ine ndinali” kapena “Ine ndidzakhala.” Iye ndi Wamuyaya, “INE NDINE!” Mwaona, “INE NDINE,” nthawizonse!

⁵⁷ Tsopano, koma Iye ankafuna kuti aziyike zinthu mu nthawi. Iye ankayenera kuti apange chinachake choti chizimupembedza, chotero zikhumbo Zake zinabereka ichi. Kenako Iye anamupanga munthu. Ndiye, mwa munthu uyu, iye ankawoneka wosungulumwa. Chotero, tsopano, kuti awonetsere tsopano malingaliro Ake aakulu, chimene Iye anali nacho mu chithunzi cha Khristu ndi Mpingo, Iye sanatenge chidutswa china cha dongo ndi kumupangira mkazi, koma Iye anatenga kuchokera kumbali ya Adamu, nthiti; ndipo anatenga kuchokera ku mzimu wa Adamu, chachikazi, ndipo anadzachiika icho mu nthiti iyi. Pamene inu mumuwona mwamuna amene akuchita ngati mkazi, pali chinachake chimene chalakwika. Ndipo pamene inu mumuwona mkazi amene akufuna kuti azichita ngati mwamuna, pali chinachake chimene chalakwika. Mwaona, pali chinachake chimene chalakwika. Iwo ndi mizimu iwiri yosiyana, pamodzi. Koma, pamodzi, iwo amapanga thunthu limodzi, “awiri awa ndi mmodzi.” Chotero Iye anamupanga mkazi ndi mwamuna, ndipo iwo sanali woti adzakalamba, sadzafa nkomwe, sadzakhala nkomwe ndi invi, nkomwe. Iwo ankadya, iwo ankamwa, iwo ankagona, chimodzimodzi monga

momwe ife timachitira, koma iwo sankadziwa nkomwe chimene tchimo linali.

⁵⁸ Tsopano ine ndizilambalala pomwe apa chifukwa cha phunziro lina nthawiina, pa mbewu ya serpenti. Chimene, iwo anandifunsa ine kuti ndizichotse zimenezo. Koma tiyeni ndimuwone winawake abwere ndipo adzandisonyeze ine chinachake chosiyana. Ndicho chimene ine ndikufuna kuti ndidziwe, mwaona.

⁵⁹ Tsopano, komano zitatha zonsezi, kenako pamene tchimo linadzalowamo, chinadzachitika ndi chiyani?

⁶⁰ Kuntunda uko, pamwamba, milioni, mamailosi handiredi milioni, kuli danga lalikulu *chonchi*, ndipo limenelo ndi chikondi cha agapao changwiro. Nthawi iliyonse imene inu mupanga sitepe yopita mbali *iyi*, ilo limachepa inchi imodzi. Ndipo inu mukudziwa mmene ilo lingadzakhalire laling'ono panthawi imene ilo lizidzafika pa dziko lapansi. Ilo ndi mthunzi wa mthunzi wa mthunzi. Ndicho chimene inu muli nacho, ndicho chimene ine ndiri nacho, mthunzi wa mthunzi wa mthunzi ya chikondi cha agapao.

⁶¹ Muli chinachake mwa inu, muli chinachake mwa mkazi aliyense muno amene wadutsa twente, muli chinachake mwa mwamuna aliyense muno amene wadutsa twente, yemwe angamafunitsitse kuti azikhilabe. Inu mwangotsala ndi zaka faifi zokha, ndizo kuchokera pa fifitini mpaka twente. Mukadutsa twente inu mumayamba kufa. Koma, kuyambira fifitini, inu mumangokhala mwana wachinyamata chabe mpaka nthawi imeneyo. Ndipo kenako inu mumakhwima mpaka mukafika twente. Ndipo mukadutsa twente, oh, inu mumati, “Ndine basi munthu wabwino.” Inu mumangonena zimenezo, koma inu simuli. Inu mukufa ndipo mukutha, ziribe kanthu kuti mukuchita chiyani. Mulungu anakupangani inu kuti mudzafike usinkhu umenewo, koma kenako inu mudzafa. Tsopano chimachitika ndi chiyani? Tsopano inu mumayamba kufa, koma mmenemo mumakhala chinachake mkati mwanu chimene chimati, “Ine ndikufuna nditakhala eyitini kenanso.”

⁶² Tsopano ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake. Nanga bwanji ngati inu mukanabadwa zaka faifi handiredi zapitazo, ndipo inu nkukhalabe moyo usinkhu wa zaka eyitini kufikira lero? Ngati inu simungakhale cha amakedzana, ndi malingaliro anu a zaka faifi handiredi zapitazo! Makolo a ammwendamnjira asanabwere konse kuno, ndipo inu nkukhala dona wamng'ono ndi mtundu wotero wa lingaliro. Bwanji, inu zikanakhala bwino mukanangopita ndi kukalamba ndi kukhala moyo zaka faifi handiredi. Mwaona, pali chinachake chimene chalakwika.

⁶³ Inu mukuti, “Chabwino, pakali pano ine ndikumverera bwino kwambiri, M'bale Branham. Oh, ndine—ndine—ine ndafika eyitini, ndine wa sikisitini, ine ndikumverera bwino.”

Wokondedwa, ndilole ine ndikuuze iwe chinachake. Iwe ukudziwa bwanji kuti amayi ako ali moyo miniti ino, ngati iwo sali mu tchalitchi chino? Iwe ukudziwa bwanji kuti bwenzi wako wamwamuna sanaphedwe maminiti pang'ono apitawo, kapena bwenzi wako wamkazi? Iwe ukudziwa bwanji kuti mmawa iwe sudzakhala mtembo mnyumba mwako? Iwe ukudziwa bwanji kuti utuluka mu tchalitchi usikuuno, wamoyo? Izo ndi zosatsimikizika. Palibepo chirichonse chotsimikizika. Ngati iwe uli fifitini, thwelofu, naintini, sevente-faivi, kapena nainte, pali. . . chirichonse ndi chosatsimikizika. Iwe sukudziwa pamene iwe ukuima. Komabe iwe umakhumba utabwerera ku fifitini, eyitini. Nchiyani chimakupangitsa iwe kuti uzichita zimenezo?

⁶⁴ Tsopano, ngati iwe utabwerera ku eyitini ndipo nkukatsalira kumeneko, ndipo osamadwalanso ndipo osati. . . iwe ungasowe kukhala ndi anthu ena ali ndi iwe, chifukwa iwe ukhoza kukula kuliposa ilo, mwaona. Anthu akhoza kumapitirira mu mibadwo inayo ndipo iwe ungakhale cha amakedzana. Iwe ungakhale utatheratu kuposa mmene izo zikanakhalira ngati iwe ukanakalamba limodzi ndi iwowo. Koma pali chinachake chimene chimakuitanira iwe kuti upite kumeneko. Chimenecho ndicho agapao yaing'ono iyo, mthunzi wawung'ono uwo umene umakupangitsa iwe. . . Chinachake chimene chiri pamwamba apa.

⁶⁵ Tsopano, usiku wina, kapena mmawa wina, seveni koloko, pamene Mzimu Woyera, mwa ubwino Wake ndi chisomo Chake, unanditenga ine kundichotsa mu thupi ili, ine ndikukhulupirira, ine ndikukhulupirira. Inde kapena ayi, ine sindikutero, ndipo ndinakalowa mdziko limenelo ndipo ndinakawawona anthu amenewo, ndipo iwo onse anali achinyamata. Ndipo ine ndinawawona anthu okongola kwambiri amene ine ndinayamba ndawawonapo mmoyo mwanga. Ndipo Iye anati kwa ine, “Ena a iwo anali a usinkhu wa zaka nainte. Iwowo ndi owatembenuza ako. Nzosadabwitsa iwo akufuula, ‘M’bale wanga! M’bale wanga!”

⁶⁶ Tsopano, limenelo ndi thupi lakumwamba, kuti pamene ife tifa ife sitimangokhala nthano, ife timasanduka thupi. Ngati ife titati, mmodzi aliyense, atafa, ngati bomba la atomiki litatiphulitsa ife pa miniti ino, mu maminiti faifi kuchokera pano ife tingakapezeke tikugwirana chanza wina ndi mzake ndipo tikukumbatirana wina ndi mzake, ndipo tikufuula ndi kumapitirira, ndi kumamulemekeza Mulungu! Inde, bwana. Ndipo M’bale ndi Mlongo Spencer wakhala apa, ine ndikuganiza limodzi la banja lakale muno, adzakakhala eyitini, usinkhu wa zaka twente. M’bale Neville angakakhale mnyamata basi, ndipo ine ndingakakhale mwana wamng’ono. Ndipo ife tonse tingakakhale basi. . . Ndizo ndendende Choonadi ichi.

“Ngati msasa wa pansi pano upasuka, ife tiri nawo wina ukudikirira kale.”

⁶⁷ Pamene khanda litsika kuchokera kwa amayi ake, ngati kubadwa kwachirengedwe, thupi lake laling’ono likuzipotokola ndipo miyendo ikulumpha, ndi zina zotero. Mundikhululukire kufotokoza kwakeko, inu akazi achichepere. Koma, pamene iye akutero, iye amakhala kuti ali ndi minyewa ya moyo ikugwadera. Koma pamene iye afika pa dziko lapansi, chinthu choyamba, iye amapuma mpweya wake, ndipo apo pamakhala thupi lauzimu la chirengedwe limene limadzalowa mwa khanda ameneyo pomwe apo. Mukamusiya yekha, iye amatenga mutu wake waung’ono ndi kuwuzika iwo pa bere la amayi ake ndi kuyamba kuyamwa. Ngati iye sachita zimenezo, mkakawo sungatuluke nkomwe.

⁶⁸ Kodi inu munayamba mwamuwonapo mwana wang’ombe pamene iye akubadwa, iye...mwamsanga akangopeza mphamvu zokwanira kuti aime pamapazi ake? Ndani amamuuzza iye? Amayenda mozungulira kupita kwa amayi ake, amayamba kuzungulira ndi kuyamba kuyamwa. Oh, eya!

⁶⁹ Pakuti, pamene msasa wa pansi pano uwu ukuberetsedwa kuno, pamakhala thupi lauzimu likukonzekera iwo. Ndipo mwamsanga pamene ili... Oh, aleluya! “Ndipo ngati msasa wa pansi pano wakukhalamo wathu upasuka, kuli wina ukudikirira uko.” Basi mwamsanga pamene ife tachoka umu, ife timakalowa mwa iwo; wina umene sufuna kumwa madzi ozizira, sumasowa kumwa madzi; wina umene sumadya, iwo si wa fumbi la pa dziko lapansi. Koma iwo ndi weniweni basi, ndipo ukhoza kukhudza ndi kugwirana chanza, ndipo basi chikondi ndi chirichonse nzangwiwo. Ndipo thupi limenelo likudikirira uko. Ili ndi gawo la ilo. Alipo atatu a iwo.

⁷⁰ Inu mumayambira Moyo wanu Wamuyaya pomwe pano pa guwa. Apa ndi pamene inu mumayambira Umuyaya. Oh! Inu mumayambira Moyo Wamuyaya pomwe apa. Mukatero inu mumabadwa mwatsopano, mwana wa Mulungu. Ndiyeno pamene inu mwafa, inu mumayamba...Pamene imfa yanu ikukanthani inu mu thupi ili ndipo mtima nkusiya kugunda, ndipo magudumu a chivundi nkuyamba kuyima nji, mthunzi waung’ono uja umene unali mthunzi wa mthunzi, mu mphindi imodzi iwo umadzakhala mthunzi wa mthunzi, kenako chotsatira iwo umadzakhala mthunzi, kenako chotsatira iwo umadzakhala kadhontho kakang’ono, kenako chotsatira iwo umadzakhala khwawa, kenako chotsatira iwo umadzakhala mtsinje, ndipo chotsatira iwo umadzakhala nyanja yaikulu, ndipo pakapita kanthawi inu mumadzakaima pamaso pa okonedwa anu atayima kumeneko, atavala zovala za thupi lakumwamba, mwakuti inu mumadziwana wina ndi mzake, mumakondana wina ndi mzake, inu mwabwereranso kukakhala ka mnyamata ndi ka mtsikana kakang’ono kenanso. Kulondola ndendende. Ilo likudikirira kumeneko kufikira kudza kwa

Ambuye Yesu. Ndipo tsiku lina thupi la ulemelero lija la Iye. . . Tsopano kumbukirani, limenelo ndi thupi lakumwamba, osati thupi laulemelero, lakumwamba. Ndipo tsiku lina thupi lakumwamba limenelo lidzachoka Kumwamba ndi Yesu.

⁷¹ “Pakuti Ine ndikunena izi kwa inu,” Atesalonika Wachiwiri, mutu wa 5, kapena Atesalonika Woyamba, mutu wa 5, uwo kapena winawo, “Ine ndinena ndi inu, ine sindikanafuna kuti mukhale osadziwa, abale, za iwo amene akugona, kuti inu musadandaule, monga enawo amene alibe chiyembekezo. Pakuti ngati ife tikhulupirira kuti Khristu anafa ndipo anawukanso tsiku lachitatu, chomwechonso iwo amene agona mwa Khristu Mulungu adzabwera nawo ndi Iye. Pakuti ife tikunena izi kwa inu mwa malamulo a Ambuye, kuti ife amene tiri moyo ndipo tatsalira kufikira kudza kwa Ambuye, sitidzawalepheretsa kapena kuwatchinga” (liwu labwino) “kuwatchinga iwo amene akugona. Pakuti lipenga la Ambuye lidzalira, ndipo akufa mwa Khristu adzauka poyamba.” Matupi akumwamba awa adzatsika pansu ndipo adzavala a dziko lapansi, matupi aulemelero. “Ndipo ife amene tiri moyofe ndipo tatsalira tidzasinthidwa mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso, ndipo tidzakwatulidwa limodzi ndi iwo, kukakumana naye Ambuye mu mlengalenga.”

⁷² “Ine sindidzamwa za chipatso cha mpesa kapena kudya kenanso kufikira ine ndidzadye izo ndi inu katsopano mu Ufumu wa Atate anga,” Mgonero wa Chikwati. Pakuti zaka zitatu ndi theka wotsutsa-khristu adzamalizitsa ulamuliro wake, dziko lonse lidzawonongedwa, Ayuda akuitanidwa atuluke, Yosefe akuzidziwitsa iyemwini kwa Amitundu, kapena kwa Ayuda. Kumbukirani, pamene Yosefe ankazidziwitsa yekha kwa abale ake, panalibepo Wamitundu mmodzi amene analipo. Pamene iye anatumiza. . . Inu mukuidziwa nkhaniyo. Yosefe, woimirira wangwiwo wa Khristu, mu khalidwe lirilonse. Ndipo pamene Yosefe anawaitanitsa abale ake, ndipo iwo nkubwera kumeneko, ndipo iye anayang’ana ndipo anamuwona Benjamin wamng’ono, ndipo iye anawawona iwo pamenepo ndipo kenako iye. . . Iwo anati, “Bwanji, munthu uyu! Ife—ife sibwenzi titamupha m’bale wathu, Yosefe.” Ayuda atawona kuti analakwitsa; tsopano pamene Khristu, pamene Iye akuzidziwitsa Iyemwini kwa iwo. Ndipo Yosefe anali atadzazidwa kwambiri, iye ankachita kulira, pafupifupi, chotero iye anamuchotsapo mkazi wake ndi ana ake, ndi azilonda onse ndi china chirichonse, ndipo anawatumiza iwo apite ku nyumba yachifumu. Kulondola ndendende. Ndiyeno pamaso pa Ayuda okha, iye anati, “Ndine Yosefe, m’bale wanu. Ndine m’bale wanu.” Ndipo kenako iwo anadzigwetsa ndipo anayamba kunjenjemera, anati, “Tsopano ife tikudziwa kuti ife tilipira izo, chifukwa choti ife tinamupha m’bale wathu. Ife tanena kuti ife tinamupha m’bale wathu, ndipo tsopano iye ndi mfumu yaikulu iyi.”

⁷³ Iye anati, “Mulungu anachita zimenezo ndi cholinga, kuti adzapulumutse moyo.” Ndicho ndendende chifukwa chimene Mulungu anachitira izo, kuti adzatipulumutse ife Amitundu. Koma Amitundu anali ku nyumba yachifumu. Aleluya! Atakanidwa ndi abale Ake, Yosefe, Iye anazitengera Mkwatibwi; ndipo Mkwatibwiyo anali wa Amitundu, osati Myuda. Chabwino.

⁷⁴ Tsopano, kodi inu mukupita kuti tsopano? Ife titavala thupi la ulemelero ili, ndi m’badwo waukulu umene uli nkudza; pamene thupi la ulemelero ili, thupi lakumwamba ili litapangidwa kukhala thupi la ulemelero. Inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza tsopano? Ndiye ine ndikhoza kuyenda ndikuti, “M’bale Neville!” Ndiloleni ine ndikuwonetseni inu pang’ono. Ine nkuti, “M’bale Humes, tiyeni tipite kwa Papa mmawa uno.” Iye ndi Mulungu. Ife tikumudziwa Iye tsopano, Iye ndi Mpulumutsi, Iye ndi Mchiritsi.

⁷⁵ Sipanayambe pakhalapo chinthu choterocho chonga kurengedwa kwa tchimo. Chimenecho sichinafike bwino pansi, sichoncho izo? Tchimo si cholengedwa. Ayi, bwana! Tchimo ndi kupotoza. Alipo Mlengi mmodzi yekha, ameneyo ndi Mulungu. Tchimo ndi chiyero chopotozedwa. Chigololo ndi chiyani? Chirungamo chopotozedwa. Bodza ndi chiyani? Choonadi choperekedwa molakwika. Ndithudi. Liwu lakuti themberero ndi chiyani? Ndi madalitso a Mulungu atatembenezidwa kukhala liwu la themberero kwa Mulungu, mmalo mokhala mdalitso. Tchimo si cholengedwa. Tchimo ndi kupotoza. Chotero, Satana sakanakwanitsa kulenga tchimo, iye ankangopotoza zimene Mulungu anali atalenga. Ndizo ndendende kulondola. Imfa ndi kupotoza chabe kwa moyo.

⁷⁶ Tsopano zindikirani izi, zindikirani izi. Kenako ine ndidzakayenda chokwera, ndipo ndizati, “M’bale Humes, tiyeni inu ndi ine, ndi M’bale Beeler ndi ena a abalewo, ife tipite kwa Papa, Mulungu. Ndipo, kuti, tiyeni tiyende ulendo pang’ono. Anyamata inu munkakonda mapiri pamene inu . . .”

“Eya, ife ndithudi tinkatero.”

⁷⁷ “Oh, alipo mamailosi milioni angapo a iwo kunja uko mu dziko latsopano ilo. Zipitani uko, kawayendeni iwo.”

⁷⁸ “Ine ndikuyenera kutero...?....dzuwa tsiku ndi tsiku, tikukwera pamwamba. Ine ndidzakumvani inu. Pamene iwo akadali chiyankhulire, ine ndidzamva.” Yesaya 66. Uko nkulondola.

⁷⁹ Ndipo inu mukudziwa, ine ndikuyenda kudutsa kumeneko, tonse a ife tikuyenda kudutsa kumeneko basi kwa pafupifupi zaka faifi handiredi, basi ulendo pang’ono, milioni, zosapanga kusiyana kulikonse, mwaona. Ndipo tsopano—tsopano zimenezo zikumveka ngati kupenga, koma ndi choonadi. Mwaona, ndicho choonadi, chifukwa sikudzakhalako nthawi, ndi Umuyaya.

Ndipo pamene ine ndidzakafika kumeneko, ine ndidzakayenda kudutsa kumeneko, ndipo inu mukudziwa yemwe ine—ine—ine ndikukumana naye kumeneko? Ine ndikuti, “Chabwino, ngati si Mlongo Georgie Bruce! Bwanji, Mlongo Georgie, papita nthawi yaitali chikuwonereni inu.” Kumawoneka monga amawonekera nthawizonse. Mukuona? Iye akhoza kukhala wausinkhu wa zaka teni milioni, koma basi kumawoneka wamng’ono basi monga amakhalira nthawizonse. Iye adzakhala akumukanda winawake ku nsana, ndipo ine kuyang’ana uko, ndi nyalugwe, mkango.

Ine nkuti, “Iwe uli bwanji mmawa uno, nyalugwe?”

⁸⁰ “Miyauu,” ngati kamphaka. “Oh, ine ndinali kumusi uko ndimayankhula ndi ena a alongo ku maluwa aakulu awo kumusi uko, ife takhala tiri kumeneko pafupifupi zaka faifi handiredi, mwaona, tikuyang’ana yang’ana.” Tsopano, izo zikumveka ngati kupenga, koma izo ndi choonadi. Ndizo ndendende. Umo ndi mmene Mulungu ankazifunira izo.

⁸¹ Chabwino, adalitse mtima wako, Mlongo Georgie. Palibe choipa chimene chingabwere, kulibe kalikonse nkomwe. Mu nthawi ya kumadzulo ife tizidzakwera pamwamba pa phiri, ndikuti, “O Papa, Mulungu, ine nthawiina ndinataika. Oh, ine nthawiina ndinali mthope la tchimo, Papa, Mulungu, ndipo Inu munandipulumutsa ine.”

⁸² Bwanji, anthu amene anayeserapo kufotokoza zimenezo anachita misala. Chabwino, munthu uja yemwe analemba ndime yomaliza ya ijayi *O Chikondi Cha Mulungu*, imene inakakhomedwa pa khoma la kwa azamisala, amene ankayesera kufotokoza chikondi cha Mulungu. Mmene Iye anazitsitsira pansu kuti adzapulumutse ochimwa, ndi mmene Iye anachitira, chikondi Chake chimene chinatsika kudzapulumutsa inu ndi ine. Mukakamba za kupembedza, Angelo samadziwa kalikonse ka izo! Kupembedza, ndi chokhacho chimene Mngelo amachidziwa. . . Iye amaima pamenepo ndi kumakupiza mapiko Ake mmbuyo ndi mtsogolo, ndi mmbali, “Aleluya! Aleluya!” Koma, oh, chifundo! Pamene zifika podziwa kuti ine ndinali wotaika ndipo tsopano ndapezeka, ine ndinali wakufa, ndiri wayoyo kenanso! O Mulungu, ine ndinali tchimo, ine ndinali thope, ndipo ine ndinali uko ku dzala!

⁸³ Apa pali chopambana chimene moyo ungatehe kukupatsani inu. Kodi inu munayamba mwapitako kumusi kuno ku dzala la Colgate? Awo ndi malo onunkhitsu amene ine ndinayamba ndafikako. Utsi wakale uwo umangondidwalitsa ine ndikawununkhiza iwo. Nditagona kumusi uko mu utsi wonse wakale uwo, nditadwalika mmimba, mukungopotokola kuchokera mkati kumatulukira panja, nditatha kumwa mafuta a msasi. Mwaona, nditadwalika basi mmene iwe ungatehere! Ndipo makoswe akungokukwera iwe, akuyesetsa kuti akudye iwe. Ndipo umenewo ndi mbambande ya moyo. Ndiyeno

winawake nkudzakufikira pansu ndi kudzakutola iwe. Ndipo iwe wakalamba kwenikweni ndipo ukulephera kuti ungasithandize wekha. Ndipo basi nkudzangokutengera iwe mmwamba ndi kukakusandutsa iwe kukhala mnyamata wasinkhu wa zaka eyitini, nkukakukhazika iwe pamwamba pa phiri, kuphukira kumene kwa thanzi, mai, kupuma kwabwino kwa mpweya watsopano monga choncho, kumamwa madzi abwino ozizira. Kodi iwe ungasunso kuti ubwerere ku dzala lija kenanso? Ayi, ayi, ayi, ayi sungapitenso ku dzala limenelo kenanso.

⁸⁴ Tsopano, ndicho chimene izo zimatanthauza, mzanga. Ndi chimene masomphenya aja, kapena kusanthulitsidwa, chirichonsecho, masomphenya. Ine ndinena kuti masomphenya, chifukwa ine ndikuwopa kuti izo zikhosha kumupweteka wina ndikanena kuti kusanthulitsidwa, ndicho chimene icho chinali. Tsopano, pamene ndi pamene Mulungu... chimene Mulungu anachita kuti awabweretse ana aamuna ndi aakazi kwa Iye. Tsopano, kodi anthu amenewa ndi ndani? Zinatheka bwanji kuti iwo... Anthu awa anachita chiyani kuti akhale owayenera izi? Iwo anachita izo motani? Mulungu, pachiyambi, Mngelo asanapangidwe nkomwe... Ndi angati amadziwa kuti Iye ndi wopanda malire? Ngati Iye siali, Iye si Mulungu. Chotero, Mulungu, mu chifundo Chake chopanda malire, Iye anawona kuti Lusifara akanadzachita zimenezo, ngati Iye alenga ichi. Iye akanadzawaika iwo pa ufulu wochita mwakufuna kwawo, maziko amenewo. Ndipo inu mukadali pomwepo, uko nkulondola, mtengo wa chabwino ndi choipa waikidwa patsogolo pa aliyense wa ife, inu mumapanga kusankha kwanu. Ndipo Lusifara anali woyambirira kutenga njira yolakwika. Ndipo iye anayamba kuzikokera kwa iye, dyera, kuyesera kudzitengera onse kwa iyemwini, kuyesetsa kuti amupitirire winawake. Ndipo apo ndi pamene izo zinayambira. Tsopano, mveterani kwa ichi. Pamene ndi pamene tchimo linayambira. Mulungu, mmalingaliro Ake opanda malire, anaziwona zimenezo, ndipo anawona kuti njira yokhayo...

⁸⁵ Tsopano, inu abale autatu, ine sindikufuna kuti ndikupwetekeni inu, koma zingatheke bwanji mu Dzina la Mawu abwino a Mulungu kuti mungamuyike Yesu kukhala munthu wapadera kwa Mulungu Mwiniwake? Ngati Yesu akanamutenga munthu wina ndi kumupanga iye kuti apite ndi kukafa, kuti adzamuwombole munthu uyu apa, Iye akanakhala munthu wosalungama. Pali njira imodzi yokha imene Mulungu akanachitira izo, ikanakhala kudzatenga malowo Mwiniwake! Ndipo Mulungu anadzasanduka thupi kuti Iye adzalawe ululu wa imfa, kuti adzachotse mbola ndi imfa kuzichotsa mwa ife, kuti ife tidzathe kuwomboledwa ndi Ake Omwe. Ndi chifukwa chake Iye azipembedzedwa kwambiri. Yesu anali munthu, ndithudi Iye anali. Iye anali munthu, m-u-n-t-h-u, wobadwa mwa namwali Maria. Koma Mzimu umene unali mwa Iye unali

Mulungu mopanda muyezo, mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mthupi. Iye anali Yehova-yire, Iye anali Yehovara-rafa, Iye anali Yehova-manasse, Iye anali Yehova; Chishango chathu, Chodzimangira chathu, Mchiritsi wathu; Iye anali Alfa, Omega, Woyamba ndi Wotsiriza; Iye anali Woyamba, Wotsiriza; Iye Anali, Amene Ali, ndipo Adzabwera; Muzu ndi Mphukira ya Davide, Nyenyezi ya Mmawa, bwanji, Iye anali Zonse-mu-zonse. Mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mthupi!

⁸⁶ Ndipo imfa nthawizonse inkakhala ndi mbola, imene inkalumira nayo anthu, “Ah,” mdierekezi amati, “Ine ndakupezeketsa iwe, chifukwa iwe wandimvetsera ine. Ndikuluma iwe, ine ndikakuika iwe mmanda. Magazi a nkhoza amenewo sangakuthandize iwe kalikonse, amenewo angokhala magazi a nyama chabe.” Koma Mulungu, mu nzeru Yake, ankadziwa kuti kukanadzabwera Mwanawankhosa, wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Inde, bwana. Ndipo iwo . . . Iye anadikirira nthawi imeneyo, kuti chidzalo cha nthawi chidzabwere.

⁸⁷ Koma tsiku lina pamene Mwanawankhosa uyu anadzabwera, Munthu uyu, ngakhale Satana anapusitsidwa. Iye anayang’ana pa Iye, iye anati, “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, panga *ichi*. Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, uchite chozizwitsa ndipo ine ndikuwone Iwe ukuchita zimenezo. Undilole ine ndikuwone Iwe ukuchita zimenezo. Uh-huh, ine ndimanga chiguduli pa nkhope Yake, nkukumenya Iwe. Ngati Iwe uli mneneri, utiuze ife amene wakumenya Iwe.” Hum! “Ine ayi, ine sindikukhulupirira kuti Iwe ndi Munthuyo. Ngati Iwe ndi ameneyo, tiwuze ife mwatchutchutchu momwe Iwe uliri.” Mwaona, zonse monga chomwecho. “Oh, tiuze ife kuti ndi Iweyo!” Iye sanatsegule kamwa Yake. Oh, oh, Iye anakokera ubweya pa maso ake ndiye!

⁸⁸ Iye anapotoloka nkuwayang’ana ophunzira, ndipo anati, “Ine ndikhoza kuyankhula kwa Atate Anga ndipo Iwo akhoza kunditumizira Ine magulu thwelofu a Angelo, ngati Ine ndikanafuna.” Pilato sanamve zimenezo, inu mukudziwa.

⁸⁹ “Ngati Iwe uli ameneyo! Ngati Iwe uli ameneyo. Oh, ameneyo si Iyeyo. Bwanji, tamuwonani Iye akuwukha magazi. Hei, ena a inu asirikali tapitani kumeneko ndipo mukamulavulire pa nkhope Yake.” Anamulavulira, anamuseleula Iye, anakamwetula ndevu zodzaza mdzanja kuchokera pa nkhope Yake. “Oh, Iye si ameneyo! Ayi, ameneyo si Iyeyo! Ine ndizika mbola yanga pa Iye, mnyamata. Ine ndikamupeza Iye pamwamba apo. Ine ndakupezeketsa Iwe tsopano!”

⁹⁰ Pamene Iye anadzalira komaliza, “Eli! Eli! Mulungu Wanga! Mulungu Wanga!” Ameneyo anali munthu. “Nchifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?”

⁹¹ Mmunda wa Getsemane, kudzoza kunamuchokera Iye, inu mukudziwa, Iye anachita kufa ngati wochimwa. Iye anafa wochimwa, inu mukudziwa zimenezo; osati machimo Ake, koma anga ndi anu. Pamenepo ndi pamene chikondi chimenecho chinadzabwerapo, mmene Iye anatengera anga! Oh, aleluya, mmene Iye anatengera anga!

⁹² Ndipo Iye anali pamenepo, Iye sanathe kutsegula kamwa Yake. Mbola inati, “Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira kuti ameneyo anali munthu wamba chabe. Iye sanali wobadwa mwa namwali, pakuti ine ndinazika mbola yanga pa Iye.”

⁹³ Ndipo ndi uyu akubwera apayu, analowetsa mbola yake pa Iye, koma imeneyo inali nthawi yolakwika, mnyamata! Iye anazula mbola yake pamenepo ndiye. Iye sangathe kubayanso kuchokera pamenepo, iye anasiya mbola yake pamenepo. Anadzauka pa tsiku lachitatu, ndipo anati, “Ine ndine Iye amene anafa, ndipo ali moyo kenanso, ndipo wamoyo kwanthawizonse, ine ndiri nawo mafungulo a imfa ndi hade.” Inde, bwana. Iye analephera kuti awone Yemwe iye anali. “Ndipo chifukwa choti Ine ndiri moyo, nanunso mudzakhala moyo. Izo sizikuwonekabe apobe . . .”

⁹⁴ Tsiku lina, masiku atatu kapena anai zitachitika zimenezo, Iye atatha kukwera kupita kwa Atate, anadzabwereranso, ndiye ena anati, “Oh, Iye ndi . . . Iye—Iye ayenera kuti ndi mzungu. Iye ayenera kukhala kuti ndi mzungu Munthu ameneyo. Ndipo ife . . . Inu mwamuwona Iye. Inu mukuona masomphenya.”

“Ayi, Iye anali Yesu weniweni.”

⁹⁵ Tomasi anati, “Ndiloleni ine ndiwone manja Ake ndi chirichonse, ine ndikuuzani inu ngati ziri zimenezo.”

⁹⁶ Iye anati, “Ndine pano.” Anati, “Inu muli ndi nsomba iliyonse ndi mkate pamenepo? Ndibweretsereni Ine sangweji.” Ndipo iwo anamubweretsera Iye sangweji, ndipo Iye anaima pamenepo ndipo anadya iyo. Anati, “Tsopano, kodi mzimu umadya mmene Ine ndikudyeramu? Kodi mzimu umakhala ndi mnofu ndi mafupa monga ine ndiri nazo?” Mukuona? Iye anati, “Ine ndine Iye. Ndine ameneyo.”

⁹⁷ Ndipo Paulo anati, “Izo sizikuwonekabe ndendende kuti ndi mtundu wani wa thupi limene ife tidzakhale nalo, koma ife tikudziwa tidzakhala ndi thupi longa Lake.” Chiyani? Kodi Iye anayamba wakhalapo ndi thupi la fiofane limenelo? Inde, bwana! Pamene Iye anafa, Baibulo limanena kuti “Iye,” ndi puronauni ya umwini aponso, “Iye anapita ku gehena ndipo anakalalikira kwa miyoyo imene inali mu ndende.” Aleluya! Iye anachita motani izo? Iye anali ndi mphamvu yokhudzira, Iye anali nazo mphamvu zakumva, Iye anali nazo mphamvu zoyankhulira, Iye analalikira ndi mtundu womwe uja wa thupi limene ine ndinawawonera okhala ndi ulemelero aja usiku wina.

Iye anakalalikirira kwa miyoyo imene inali mu gehena, imene siinalape mu kupirira kwa masiku a Nowa.

⁹⁸ Koma pamene Iye anadzauka pa Isitara, izo sizikanatheka kuti thupi limenelo liwone chivundi, chifukwa Davide mneneriyo anawoneratu izo, “Ine sindidzasiya solo Yake mu gehena, komanso sindidzalola Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi. Komanso thupi Langa lidzapuma mu chiyembekezo, chifukwa Iye sadzasiya solo Yanga mu gehena, komanso Iye sadzasiya Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi.” Ndipo pa maora sevente-thuu chivundi chisanalowe, fiofane ija, thupi lija limene linapita ndi kukalalikirira kwa miyoyo imene inali mu ndende, imene siinalape mu kupirira kwa masiku a Nowa, inauka kachiwiri, ndipo chivundi chinavala chisavundi, ndipo Iye anaimirira ndipo Iye anadya, ndipo Iye anatiuza ife kuti Iye anali Munthu. Aleluya!

⁹⁹ Umo ndi mmene ife tidzamuwonere Iye, M'bale Evans. Pamenepo ndi pamene Iye ati adzakhale pa mpando wachifumu wa Davide. Aleluya! Pamenepo ndi pamene ife tizikayenda chokwera ndi chotsika tsopano, ine ndizikayenda ulendo ndi inu kudutsa mmapiri kwa zaka milioni, mwaona, masiku pang'ono chabe, maminiti pang'ono chabe, ife tizidzapita kukadutsa kumeneko, kukakhala mozungulira pamenepo.

¹⁰⁰ Ndipo ikafika nthawi yakudya, inu mukudziwa, chinthu choyambirira inu mukudziwa, Mlongo Wood akati... Ine ndikati, “Mlongo Wood, chabwino, inu mwakhala muli kuti nthawi yonseyi? Ine sindinakuwoneni inu kwa... zikuwoneka kwa ine ngati akhala ali maminiti fifitini.”

“Oh, zimenezo ndi zaka thuu sauzande zapitazo, M'bale Branham.”

¹⁰¹ “Uh-huh. Inu mukumverera bwanji?” Oh, ndithudi iwe sungamverere chinanso koma mwabwino.

¹⁰² “Nkuti, bwerani kuno, anyamata, ine ndikuwonetsani inu nonse chinachake, abale, abale anga okondedwa. Apa pali kasupe wa madzi apa, opambana amene inu munayamba mwamwapo. Ndipo, oh, ife nkumwa madzi abwino ozizira. Ine ndidzakafikirira pamenepo ndi kutengapo chiphava chachikulu cha mphesa, ndipo ife tonse nkukhala pansu pamenepo ndi kumadya izo.” Kodi zimenezo sizikakhala zodabwitsa? Ndizo ndendende chimene izo ziri. Ndi zimenezo basi.

¹⁰³ Ife tinazipeza chotani izi? Ife timazidziwa bwanji izo? Mulungu, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, anatikonzeratu ife! Ndani? Iwo amene ali mu Dziko lonjezedwa.

... anatikonzeratu ife ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu... mogwirizana ndi ubwino wake wa chifuniro chake.

Kwa matamando a ulemerero Wake . . .

Kuti ife tizidzamupembedza Iye monga Iye ananenera. Ndicho chimene Iye anali, Mulungu. Ife tikufuna kumupembedza Iye.

. . .matamando a ulemelero wake wa chisomo chake, mmene iye watipanga ife ovomerezeka mwa wokondedwa. Mwa Khristu ife timavomerezedwa.

Mwa yemwe ife tiri nacho chiwombolo kudzera mu magazi, chikhululukiro cha m-a-c-h-i-m-o . . .

¹⁰⁴ Ine ndikuyenera kuti ndibwerere ku kukhazikitsidwa, koma ine ndikufuna kuti ndiimire pa “machimo” apa miniti. “Machimo,” kodi inu munazindikira zimenezo? Inu mukudziwa Mulungu samamuweruza wochimwa chifukwa chochimwa? Iye amamuweruza iye chifukwa chokhala wochimwa. Ngati wochimwa akusuta ndudu, Iye samuweruza iye chifukwa cha izo; iye ndi wochimwa, mulimonse. Mukuona? Mukuona? Iye alibe machimo aliwonse, wochimwa samakhala nawo. Iye ndi wochimwa basi, mwaona, iye alibe machimo aliwonse. Koma inu mumakhala ndi tchimo, inu amene muli Akhristu. Inu mukuzindikira apa iye akuyankhula kwa Mpingo. Akumuika iye mowongoka. Mukuona? Mukuona? “Chikhululukiro cha machimo,” m-a-c-h-i-m-o. Ife timachita tchimo. Koma wochimwa amangokhala wochimwa basi, Mulungu samamukhululukira iye.

¹⁰⁵ Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, iye anapita kunja uko ndipo anakamuwombera munthu. Inu muchita chiyani ndi izo?” Imeneyo si ntchito yanga. Ine si wokonzanso, ndine mlaliki. Lamulo lidzasamalira zimenezo, iwo ndi okonzanso. Iwo ali. . . “Chabwino,” mukuti, “iye anachita chigololo.” Izo, izo—zimenezo ndi zokhudza lamulo. Zimenezo ndi za pakati pa iye ndi lamulo. Ine—ine—ine—ine si wokonzanso, ine sindimawakonzanso anthu. Ine ndimafuna kuti iwo atembenuke. Ndine mlaliki, mwaona, ntchito yanga ndi kumutengera iye kwa Mulungu. Ngati iye anachimwa, imeneyo ndi ntchito yake, iye ndi wochimwa. Mulungu amamuweruza iye pa muyezo wapamwamba. Iye ndi wochimwa kuyamba ndi kuyamba, iye ndi woweruzidwa kuyamba ndi kuyamba. Iye sanafike nkomwe pa maziko oyambirira, iye—iye—iye palibepo paliponse. Iye ndi wochimwa kuyamba ndi kuyamba. Iye alibe machimo aliwonse, iye ndi wochimwa.

¹⁰⁶ Inu simungapite kunja ndikumati, “Kuchuluka *chomwechi* ndi usiku, ndipo kuchuluka *chomwechi* si usiku.” Ayi, wonsewo ndi usiku, basi wonsewo ndi usiku. Ndicho chimene Mulungu ananena. Uko nkulondola, iye ndi wochimwa basi, ndizo zonse. “Tsopano, iye wachita ichi, *mmene* wachulukiramu ndi usiku, *wvu* ndi usiku wowala kwenikweni apa.” Ine ndikudziwa, koma iwo wonse ndi usiku, ndizo zonse. Mukuona?

107 Ine sindinganene kuti, “Kuchuluka *chomwechi* ndi kuwala pomwe apa.” Ayi, konseko ndi kuwala, mwaona, kuwala basi, inu simungati kukachuluka chonchi. Mukuona? Koma ngati iye ali malo akuda *apa*, ndiye kuti pali mdima pamenepo.

108 Chotero “machimo,” m-a-c-h-i-m-o, ife tiri nacho chikhululukiro cha machimo athu kudzera mu (chiyani?) Magazi Ake, Magazi ofunika.

... *monga mwa kulemera kwa chake* ...

109 Ife timaiwala chotani izo? Chifukwa ndife oyenera, ife tinachita chinachake kuti machimo athu akhululukidwe? Chiyani Chake?

... *chisomo*;

110 Oh, mai! Palibe kalikonse mmanja mwanga kamene ndikubweretsa, Ambuye. Palibe chomwe ndingachite, palibepo chinthu chimene ine ndingachite. Penyani! Iye anandikonzeratu ine, Iye anandiitana ine, Iye anandisankha ine. Ine sindinamusankhe Iye. Iye anandisankha ine, Iye anakusankhani inu, Iye anatisankha ife tonse. Ife sitinamusankhe Iye. Yesu anati, “Inu simunandisankhe Ine, Ine ndinakusankhani inu.” Iye anati, “Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba, ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine. Ndipo palibe aliyense wa iwo ati adzatayike, kupatula mwana wachitaiko, kuti akwaniritse a—Lemba.” Inu mukuona? Anati, “Koma onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine.”

111 Oh, ine ndikuchedwetsa kwambiri, sichoncho ine? Ndipo ine sindinachokebe mu izi. Ine sindinayambebe pa izi. Ndiloleni ine ndifulumire, ine ndikuyenera kuti ndifike kwa chinachake pomwe apa mwamsanga basi tsopano, ndipo ife tifulumire. Ine ndikuyenera kuti ndibwerere ku kukhazikitsidwa uku miniti chabe. Oh, kodi inu mungandikhulukire ine basi kwa—kwa miniti yokha? Tiyeni titenge izi apa, ena a anthu awa achokera njira yonse ku Georgia kubwera kuno kwa usikuuno wokha, adalitse mtima wawo. Tsopano, m’bale Georgian, ndi Texas ndi kulikonse kumene inu mukuchokera, mvetserani ndime ya 5 iyi. Tiyeni tichedwepo pa iyo maminiti pang’ono.

Anatikonzeratu ife ku—ku ...

112 Kodi mawu akuti “ku” amatanthauza chiyani, mawu akuti “ku”? Iwo amatanthauza chinachake kumene ife tikupitako, ku. “Ine ndikupita ku kasupe. Ine ndikupita ku mpando.” Humes, iwe ukumvetsa zimenezo? “Ine ndikupita ku tebulu.”

Tsopano, Iye anatikonzeratu ife ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa iyemwini, monga mwa kufuna Kwake Komwe kwabwino kwa chifuniro chake,

113 Kufuna kochulukwa bwanji? Kufuna kunali kwa ndani, ubwino wa ndani? Wake Womwe. Kufuna Kwake Komwe kwa Iye kwa Chifuniro Chake Chomwe!

114 Tsopano, kodi “kukhazikitsidwa” ndi chiyani? Tsopano mundilole ine nditenge izi tsopano, ine sindikudziwa ngati. . . Ine sindikhala ndi nthawi yoti ndimalizitse izi, koma ine ndizigunda izo. Ndiye ngati pali funso, inu mukhoza kudzandifunsa ine mtsogolo pang’ono nthawiina mu uthenga, chinachake. Mvetserani. Kukhazikitsidwa kwanu si kubadwa kwanu. Kukhazikitsidwa kwanu ndi kuyikidwa mmalo kwanu. Pamene inu munkabadwa mwatsopano, Yohane 1:17, ine ndikukhulupirira, pamene ife tibadwa mwa Mzimu wa Mulungu, ife timakhala ana a Mulungu. Koma ife tinakonzedweratu. Tsopano ndi ichi chimene ine ndikufuna ndikufikitseniko inu, cha ana awa a tsiku lotsiriza, inu mwaona. Kuti. . . Mukuona? Ife tinakonzedweratu ku (kwa) kukhazikitsidwa.

115 Tsopano, tsopano ndife apa. Tsopano, ichi ndi chimene chimawapweteka a Chipentekoste pang’ono. Iwo amati, “Ine ndinabadwa mwatsopano! Ambuye alemekezeke, ndinalandira Mzimu Woyera!” Zabwino. Ndinu mwana wa Mulungu. Uko nkulondola. Komabe zimenezi si zimene ine ndikuzikamba. Mwaona, inu munakonzedweratu ku kukhazikitsidwa. Kukhazikitsidwa, ndi kumuyika pamalo mwana.

116 Ine ndayandikira kwambiri kwa chimenecho, chifukwa Becky amandiuza ine kuti ndikumayandikira kwambiri kwa icho, inu mukulephera kundimva kumbuyoko. Ine ndi. . .

117 Mwaona, mwana. Ndi angati amene amadziwa malamulo a kukhazikitsidwa mu Chipangano Chakale? Ndithudi, inu mwaziwonapo. Mwana akabadwa. Ine ndikukhulupirira ndinali nazo izo mu ulaliki wina. Ndi chiyani iwo, Gene, iwe ukukumbukira? Izo ziri pa tepi. Oh, unali chiyani iwo? Ine—ine—ine—ine ndinakhudzapo pa izo. Oh, eya, ine ndawupeza, *Mvereni Inu Iye*. *Mvereni Inu Iye*; kukhazikitsidwa kwa ana.

118 Tsopano, mu Chipangano Chakale, pamene a—pamene mwana abadwa mu banja, iye amakhala mwana pamene iye wabadwa, chifukwa iye amabadwa mwa makolo ake, iye amakhala mwana wa banjalo ndi wolowa wa zinthu zonse. Tsopano, koma mwana uyu amaleredwa ndi aphunzitsi. Agalatiya, mutu wa 5, ndime ya 17 mpaka ya 25. Chabwino. Iye amaleredwa ndi aphunzitsi, olera, aphunzitsi. Tsopano, mwachitsanzo, ngati ine nditakhala ndi mwana yemwe wabadwa, kuti, ndine bambo ndipo. . .

119 Ndipo ndi chifukwa chake mu King James, ndi angati anayamba aganizapo kuti zimamveka moseketsa mu Zolemba za King James, amati, “Mu nyumba ya Atate Anga muli nyumba zazikulu zambiri”? Nyumba, nyumba zazikulu zambiri. Mukuona? Kwenikweni, mu—mmasiku amene Baibulo

ankamumasulira King James, *nyumba* inali “ulamuliro.” “Mu *ulamuliro* wa Atate anga muli nyumba zazikulu zambiri.” Osati mnyumba, nyumba zazikulu, koma Iye ankatchedwa Atate wa ulamuliro uwu. Iwo ankakhala nazo izo mwa Baibulo kwambiri, mu Baibulo ndi momwe izo zinkakhalira.

¹²⁰ Pamene bambo akhala ndi munda waukulu wa maekara sauzande, kapena chinachake chimzake, iye amakhala ndi gulu la anthu amene amakhala *kuno*. Iye amakhala ndi manja antchito amene amakhala *kuno* kuti azisamalira nkhosazo, iye amakhala ndi ena *kuno* oti azisamalira ng’ombe, iye amakhala ndi ena *kuno* amene ankapita ku chandamale kumtunda uko kutalika mamailosi handiredi, ndipo iye amakhala ndi ena pomwe apa *kuno* osamalira mbuzi, ndipo iye amakhala ndi ena osamalira mphongolo ndi—ndi zinthu zosiyanasiyana. Iye—iye basi anali ndi ufumu waukulu. Ndipo iye amakwera pa bulu wake wamng’onyo ndipo iye amakwera kumazungulira kupita kwa aliyense ndi kukawawona momwe iwo akugwirira ntchito, kumweta ubweya wa nkhosa ndi chirichonse monga choncho. Iye samakhala ndi nthawi . . .

¹²¹ Inu simukundimva ine ndikachokapo pamenepo. Ine—ine—ine ndiyetsa kukhala kumbuyo kuno. Kodi inu mukukhoza kundimva ine bwinobwino tsopano, apa? Penyani.

¹²² Iye amakwera nkumapita, ndipo amapita kutali, kuyetsa kuti—kuti asalimire wake—wake—ufumu wake. Chotero tsopano iye amafuna . . . Mwana ameneyo adzakhala wolowa wa chirichonse chimene iye ali nacho. Iye ndi wolowa.

¹²³ Ndipo pamene iye tibadwa mu Ufumu wa Mulungu, mwa Yesu Khristu, ife timakhala olova a Kumwamba, olova limodzi ndi Yesu, chifukwa Iye anadzatenga malo athu. Iye anadzakhala ife (tchimo), kuti ife tidzakhoze kukhala Iye (chirungamo). Mukuona? Iye anadzakhala ine kuti ine ndidzakhoze kukhala Iye, mwaona, olova limodzi ndi Iye. Chabwino, tsopano mukumbukire zimenezo, kwa aliyense wa inu.

¹²⁴ Tsopano, kumbukirani, Mulungu anakukonzeranitu inu, mwa kudziwidwiratu, kuti inu munkabwera ku Ichi. Aliyense amene akumvetsa zimenezo, kwezani dzanja lanu, mwaona. Mulungu, mwakudziwiratu, anakukonzeranitu inu kuti mudzabwere ku Dziko lolonjezedwa. Kodi Dziko lolonjezedwa la Mkhristu lero ndi chiyani? Mungokweza mmwamba dzanja lanu ngati inu mukudziwa. “Lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu, kwa iwo amene ali kutali. Ndipo zidzachitika mmasiku otsiriza, atero Mulungu, kuti ine ndidzatsanulira cha Mzimu Wanga pa mnofu wonse, ana anu aamuna ndi ana anu aakazi.” Ndipo mu Yesaya 28:18, “Lamulo likhale pa lamulo, mzere pa mzere; apa pang’ono, apo pang’ono. Mugwiritsitse icho chimene chiri chabwino. Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ine ndidzayankhula kwa anthu awa. Ndipo uwu ndi mpumulo,

(a—Mpumulo) dziko la sabata limene ine ndinanena kuti iwo adzalowemo. Ndipo, pakuti zonsezi, iwo samazimva, koma iwo anagwedeza mitu yawo ndi kuchokapo, ndipo sanazimve Izo.” Mukuona? Ndendende.

¹²⁵ Chinali chiyani chimenecho? Basi ndendende monga anthu aja amene anabwera njira yonse kuchokera ku Kenani, kapena kuchokera ku Igupto, njira yonse chokwera kudutsa mu chipululu, ndipo anadzafika moyandikira, pafupi kwambiri kuti adzalawe mphesa zimene zinkachokera mdzikolo. M'bale, pamenepo, anthu amenewo akufuna kuti ine ndibweze zimenezo, zimenezo ziri pa Ahebri 6. Ine ndingachithe bwanji zimenezo? Amenewo ndi okhulupirira a mmalire, iwo sadzapitako uko nkomwe! Iwo sangathe kupitako. Yesu anatero.

Iwo anati, “Makolo athu ankadya manna mchipululu.”

¹²⁶ Ndipo Yesu anati, “Iwo ali, mmodzi aliyense, anafa.” Amene analakanitsidwa. Iwo ali, mmodzi aliyense, anafa. Uko nkulondola. Anati, “Koma Ndine Mkate wa Moyo umene unabwera kuchokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba. Munthu amene adya Mkate uwu, iye sadzafa konse. Uko nkulondola. Inde, bwana, iye akhala nawo Moyo Wamuyaya ngati iye adya Uwu, Ndine Mtengo uwo wa Moyo wochokera mmunda wa Edeni.”

¹²⁷ Tsopano, onani, anthu awa unabwera pafupi kwambiri! Mwaona, ngati inu mungazindikire mu Ahebri 6, osati kubwerera ku zimenezo, koma mu Ahebri 6, “Anthu awa amene anapangidwapo kukhala otenga nawo, anabwera pafupi kwambiri, ndipo analawa nawo za mphatso ya Kumwamba.” Iwo anakhala nawo pamenepo, iwo anawona machiritso akuchitika, iwo anawawona anthu ali mu mphamvu ya Mulungu, iwo anaiwona miyoyo ikusinthika, koma iwo akulephera kuika dzanja pa Iwo. Ayi, bwana. Ayi, bwana. “Ndipo analawa mphamvu ya dziko limene liri nkudza; ndipo ngati iwo ayesera kuzikonza okha kenanso ku kulapa, powona kuti iwo—kuti iwo adzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu kachiwiri, ndipo awayesa Magazi a pangano amene iwo anayeretsedwa nawo. . .”

¹²⁸ “Ine ndi wa mpingo umene umakhulupirira mu kuyeretsedwa.” Zimenezo ndi zabwino mmene izo zikupitira, koma inu simupita patali mokwanira. Mukuona? Inde, bwana. Chipululu chinawayeretsa iwo. Inde, ndithudi. Iwo anali a—iwo anali ndi njoka ya mkuwa ndi a—guwa la mkuwa, ndi chirichonse kunjira uko, kuyeretsedwa, koma iwo anakalowa mu Palestina kuti akapumule. Sanati. . .

¹²⁹ Muyang'anenso mu Ahebri 4, kodi iye sanati “Mpumulo wina”? Mulungu analenga tsiku la chisanu ndi chiwiri ndipo anawapatsa iwo mpumulo pa tsiku la chisanu ndi chiwiri. Malo ena iye anayankhula za tsiku la mpumulo, “ndipo lero mwa

Daive.” Kenako Iye anawapatsa iwo Mpumulo wina, “Idzani kwa Ine inu nonse olema ndi othodwa, Ine ndidzakupatsani inu Mpumulo.” Lowani mu Mpumulo uwu! Pakuti ife amene talowa mu Mpumulo uwu tapuma ku ntchito zathu monga Mulungu anachitira kwa Zake pa sabata. Ndithudi. Ndi imeneyo sabata yanu, Mpumulo. Ndi umenewo Mpumulo wanu weniweni mu Dziko lolonjezedwa ili.

¹³⁰ Mzimu Woyera ndi lonjezo la anthu. Ndipo nchifukwa chiyani iwo amafuna alaliki ophunzira amene amawalola iwo kumavala akabudula ndi kudula tsitsi lawo, ndi kumapenta mmilomo, ndipo mwamuna amene amachita njuga ndi kumwa mowa ndi kumanena nthabwala, ndi kumapitirira ndi kumapitirira monga choncho, ndipo nkumadzitcha okha mamembala a mpingo? Bwanji, iwo amatenga chinachake chonga chimenecho ndi kukana utsogoleri wa Mzimu Woyera! Bwanji, Baibulo linati Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse limene limadula pakati fupa, ndipo ngakhale wozindikira malingaliro a mtima. Inde, ngakhale malingaliro a mmaganizo!

¹³¹ Ndipo ngati ife tilikonda dziko lapansi kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa ife. “Ambiri aitanidwa, apang’ono asankhidwa; pakuti khwalala ndi chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza yopita ku Moyo, ndipo koma ochepa adzakhalapo amene ati adzaipeze iyo. Ambiri adzadza kwa Ine mu tsiku limenero ndipo adzakhalala pansu mu Ufumu,” anatero Yesu, “ndi Abrahamu, Isaki ndi Yakobo. Koma ana a ufumuwo adzaponyedwera kunjja, ndipo adzati, ‘Ambuye, kodi ife sitinachite izi mu Dzina Lanu? Kodi ife sitinalalikire? Kodi ife sitinakhale Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* ndi M’busa *Wakuti-ndi-wakuti*?’ Ine sindinakudziweni inu nkomwe. Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaeruzika, ine sindinakudziweni inu. Si onse amene anena, ‘Ambuye, Ambuye,’ adzalowamo. Koma iye amene akuchita Chifuniro cha Atate Anga amene ali Kumwamba, ameneyo ndi amene ati adzalowe.”

¹³² Ndi zimenezotu, kulowa mu Dziko lolonjezedwa ili. Ife timalowamo chotani mmenemo? Ife tinakonzedweratu kwa ilo. Mpingo, mwa kudziwidwiratu kwa Mulungu, unakonzedweratu (kwa chiyani?) kwa ulemu Wake, mwa chisomo Chake, kwa ulemelero, ndi kupembedza ndi ulemelero wa Mulungu. Papa, atakhala kumbuyo uko pachiyambi, wokhalapo-yekha, wopanda kalikonse pomuzungulira Iye, ankafuna chinachake choti chizidzamupembedza, chotero Iye anadzodzeratu ndipo anawukonzeratu mpingo, ndipo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndipo anaika maina awo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, pamene iwo . . . wophedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, kuti iwo adzathe kuwonekera kwa ulemelero Wake ndi kwa matamando Ake pamapeto a nthawi, pamene adzasonkhanitsa zinthu zonse mwa Munthu mmodzi

ameneyo, Khristu Yesu. Psyii! Ulemelero! Ndi zimenezotu. Ndizo basi . . . Ndipo ndi zimenezo pomwe apo, m'bale wanga, mlongo. Inu musadzachoke konse kwa Izo.

¹³³ Mulungu, mwa chisomo Chake chosankha, anakuitanani inu. Mulungu, mwa chisomo Chake chosankha, anakuyeretsani inu. Mulungu, mwa chisomo Chake chosankha ndi mphamvu Yake, anakubatizani inu ndipo anadzakuikani inu mdziko ili la Mpumulo. Iwo amene analowa mu Mpumulo uwu apuma ku kusochera kwawo. Iwo anapuma ku ntchito zawo monga Mulungu anachitira ku Zake. Iwo ali ndi chimwemwe chosaneneka, ndipo chodzaza ulemelero! Mtengo wa Moyo ukuphukira mwa iwo. Iwo ali ndi kulezamtima, chifundo, ubwino, chipiriro chopangidwa kukhala chikhulupiriro, chikhulupiriro, chifatso, chifundo, ndi zina zotero. Mtengo wa Moyo ukuphukira mwa iwo chifukwa chiyembekezo chawo chazikika mwa Khristu Yesu, mboni ya Mzimu Woyera kumachitira umboni ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwatsatira okhulupirira. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Pamene iwo akupitirira, iwo akuchiritsa odwala, iwo akutulutsa ziwanda, iwo akuyankhula ndi malirime, iwo akuwona masomphenya. Iwo . . . Ndipo iwo akuyenda ndi Mulungu, iwo akuyankhula ndi Mulungu. Palibe mdierekezi amene angawasunthe iwo, iwo ndi okhazikika, akuyembekezera . . . ? . . . Kuiwala zinthu izo zakale, iwo akukakamira kufika ku malo akuitana kwapamwamba mwa Khristu Yesu. Ndi amenewotu. Ndi amenewotu. Ndi umenewo Mpingo.

¹³⁴ Iwo anafikako bwanji kumeneko? Inu simunganene kuti, “Chabwino, Ambuye, Inu mukudziwa, tsiku lina ine ndinayamba kusuta ndudu, ndipo ine ndinagwa, kenako ine ndinaganiza ine ndi . . .” Oh, ayi, ayi, ayi, ayi.

¹³⁵ Kukonzedweratu! Iye anatiitana ife ndipo pamene ife tinamutsatira Iye ndi pamene ife timati, “Mulungu, ife tinataika ndipo tinathedwa. Ife tinalibe nkomwe malingaliro oti tingadzipulumutse tokha. Ife tinali chikhaliidwe cha nkhumba, ife tinali nkhumba kuyamba ndi kuyamba.”

¹³⁶ Inu mupite ku khola la nkhumba ndipo mukaiwone nkhumba yaikazi yokalamba, ndipo mukati, “Tsopano, tayang’ana apa, mtsikana wokalamba, ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe chinachake. Izo ndi zoipa kuti iwe uzimwa zithaphwi.”

¹³⁷ Iyo ikhoza kunena kuti, “Onki-onki.” Mukuona? Tsopano, izo ndi kuchuluka kwa zimene iwe uli nazo zoti uzipulumutse iwemwini. Ndizo ndendende.

¹³⁸ Inu mukuti, “Dona, inu musamavale zovala monga choncho, inu muzivala mowoneka bwino. Inu muzichita *izi*. Inu musamapite ku . . . Inu musamakhale ndi maphwando a makhadi

awa. Inu musamasute ndudu. Inu musamachite *izi*. Bambo, inu musamachite *zimenezo*.”

¹³⁹ Iye amati, “Onki-onki. Ine ndi wa *Onki-onki*.” Uh-huh. “Onki,” ndizo basi kuchuluka kwa zimene iwo amazidziwa. “Chabwino, ine ndikudziwitsani inu kuti ndine wabwino basi monga mmene inu muliri. Onki-onki!” Mwaona, iwo amakana utsogoleri wa Mzimu Woyera, pakuti Baibulo linanena kuti ngati inu mukonda dziko lapansi kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.

¹⁴⁰ Nchiyani chimawapangitsa iwo kukhala achirendo? Inu ndi fuko loyera. Kodi inu munachita chiyani? Munalowa kutuluka mdziko limenelo. Inu munakalowa mu Dziko lina. Inu munapitako bwanji kumeneko? Limenelo ndi Dziko lolonjzedwa. Ndi lonjezo la mtundu wanji? “Zidzachtika mmasiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa thupi lonse.” Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Dziko limodzi lolonjzedwa ili. Ameni. Abale ndi alongo, aleluya, ndi ungwiro wa mtima, opanda nsanje, opanda udani, opanda kalikonse! Ine sindikusamala kaya m’bale walowerera, ziribe kanthu zimene iye akuchita, inu mumutsatire iye.

¹⁴¹ Ine ndinamutsatira m’bale osati kale kwambiri, amene analowelera. Mnyamata anati kwa ine, anati, “Musiyeni mthakati ameneyo azipita. Musiyeni iye yekha.”

¹⁴² Ine ndinati, “Ngati ine ndingadzafike konse pa malo amene mtima wanga sukugwirizana ndi m’bale wanga, ndiye ndi nthawi yoti ine ndipite paguwa, chifukwa ine ndagwa kuchokera pa chisomo.” Ine ndinati, “Ine ndidzapita bola ngati iye ali ndi mpweya mthupi lake, ndipo ine ndidzakamugwira iye penapake mu mzerewo.” Inde, bwana. Ndipo ine ndinakamupeza iye, aleluya, ndinamubweretsanso iye. Inde, bwana. Iye anabwerera mkhola motetezeka tsopano. Inde, bwana. Iye akanalowerera motsimikiza basi monga dziko.

¹⁴³ Kanthawi kapitako pamene ine ndinamuwona mkazi wosauka wamng’ono uja atakhala pamenepo, ndipo apolisi nkundiitana ine, anati, “Bwanji, iye akuyenera kuvala malaya athumba.” Anati, “Iye wapenga basi, iye wazungulira mutu.” Iye—iye, iwo anakamuika iye mu hotelo. Iwo anabwera.

Ine ndinati, “Izo ziri bwino.”

¹⁴⁴ Anati, wapolisi anati, “Bwanji, Billy!” Ine ndikumudziwa iye bwino bwino, ndipo ndikumudziwa iye kuyambira ine ndiri mwana. Iye anati, “Ngati pali chirichonse chimene ine ndingapange kuti ndikuthandizeni inu.”

Ine ndinati, “Izo ziri bwino.”

Anati, “Kodi inu mungamuthandize iye?”

Ine ndinati, “Ayi, koma *Iye* akhoza.” Ine ndinati, “Miniti chabe.”

¹⁴⁵ Chotero iwo anamubweretsa iye kumeneko. Ndipo pamene iye amachoka kanthawi kapitako, mu mtendere. Chinali chiyani chimenecho? Ife tinatumiza pemphero kuti limutsatire iye. Amen! Iye anali kwambiri. . .

¹⁴⁶ Iwo anati, “Kodi inu mukufuna mupeze dokotala?” Anati kwa mwamuna wake, “Kodi inu mukufuna kupeza dokotala?”

¹⁴⁷ Anati, “Dokotala sangamuthandize iye kalikonse.” Ndipo izo nzoona. Iye wachita wamisala; dokotala sangamuthandize iye kalikonse.

Ndinati, “Chiyembekezo chatu chokhacho ndi kupita *kumeneko*.”

Ndipo iye anati, “Billy, ine sindikumvetsa zimenezo.”

Ine ndinati, “Ine sindikuyembekeza kuti iwe ungatero, mwaona. Sindikuyembekeza kuti ungatero.”

¹⁴⁸ Koma, oh, mai, inenso sindimazimvetsa izo! Ayi. Koma, m’bale, Mulungu Kumwamba. . . ine ndinali kutali, kunja uko nthawi ina, Chinachake chinanditsatira ine. Amen! Ichosichinali chifukwa choti ine ndinkafuna kubwera, koma, ayi, Chinachake chinanditsatira ine. Chifukwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, Mulungu anakonzeratu, aleluya, kuti ife tidzakhale Ake, kwa ulemu Wake ndi ulemelero. Mvetserani! Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye watani? Wawaitana. Kulondola uko? Kodi Iye anakuitanani inu? Eya! Nchifukwa chiyani Iye anakuitanani inu? Iye anakudziwiranitu inu. Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana; iwo amene Iye wawaitana, Iye wawalungamitsa. Nkulondola uko? Ndipo iwo amene Iye wawalungamitsa, Iye wawapatsa ulemelero! Amen! Ndicho chimene Baibulo limanena. Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana. Kam’badwo kalikonse! Iwo amene Iye anawaitana, Iye anawapatsa kale ulemelero. Chiyani? Ndiloreni ine ndiwerenge Lemba apa. Chabwino.

Anawakonzeratu iwo ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa iyemwini, monga kunankomera Iye Mwini. . .

Kwa matamando a ulemelero Wake. . .

¹⁴⁹ Oh, kodi inu mukumvetsa zimenezo? Kwa matamando a ulemelero Wake! Kuti Iye adzakhale pamenepo mu mibadwo Yamuyaya imene iti iyambike, ndipo ana Ake azidzafuula, “Abba, Atate! Abba, Atate!”

¹⁵⁰ Ndipo Angelo azidzati, “Kodi iwo akuti chiyani? Kodi iwo akuti chiyani?”

¹⁵¹ Zinawonetseredwa mokongola mwa mwana wolowerera. “Ine ndinataika.” “Uyu ndi mwana wanga. Iye anataika

ndipo tsopano wapezeka. Iye anali wakufa, ndipo ali moyo kenanso. Bweretsani mwana wa ng'ombe wonenepayo, mwinjiro wapamwamba, mphete ndipo muiveke iyo pa chala chake. Ndipo tiyeni. . .” Nzosadabwitsa pamene nyenyezi za mmawa zinkaimba pamodzi, ana aamuna a Mulungu anafuula ndi chimwemwe, pamene iwo anawona dongosolo la chipulumutso, Mulungu akuyika dzina lanu pa Bukhu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.

¹⁵² Tsopano inu mukuti, “Kalvin anakhulupirira chinachake chonga chimenecho.” Ine sindinamukhulupirire Kalvin. Kalvin anali wakupha. Kalvin anamupha munthu chifukwa choti iye anabatiza mu Dzina la Yesu. Iye anali mthakati, ankasowejera kuti atembenezidwe, iyemwini. Inde, bwana. Koma zimene iye ananena, za zinthu zina zimene iye ananena, zinali zolondola. Musati. . .koma zimene iye. . .Zochita zake, munthu amene angaphe munthu chifukwa cha chinachake chonga chimenecho, izo ndi zowopsya, izo ndi utchimo. Chabwino.

Mmene iye wachulukitsa kwa ife. . .

¹⁵³ Oh, dikirani, ine sindinatenge chijachi “kukhazikitsidwa,” ine ndinatenga? Ine ndachedwa kwambiri? Tiyeni tiwone chimene wotchi iyi ikunena apa, nthawi imene ife tiri nayo. Chabwino. Basi—tiyeni tingotenga maminiti teni chifukwa cha anthu awa amene achokera kutali. Onani. Onani.

¹⁵⁴ “Kukhazikitsidwa,” ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chifukwa chimene izo zimachitikira tsopano. Abambo ali ndi ufumu waukulu, iye amakwera nkumazungulira. Tsopano ali ndi mwana amene wabadwa. Oh, iye ndi wokondwa kwambiri! (Ameneyo ndi Mulungu.) Chotero inu mukudziwa chimene bambo ameneyo amachita? Iye amakampeza wolera wabwino kwambiri, mphunzitsi. Inu mukudziwa kuti mphunzitsi ndi ndani, si choncho inu? Ndi mphunzitsi wa ku sukulu. Iye amakapeza mphunzitsi wabwino kwambiri amene iye angamupeze mdziko lonse. (Ndiyeno ife tikupita tsopano, mvetserani.) Ndipo iye amakampeza mphunzitsi wa sukulu wabwino amene angamupeze. Iye samangotenga chigawenga, iye amafuna mnyamata wake kuti adzakhale mnyamata weniweni.

¹⁵⁵ Kodi inu simumafuna ana anu adzakhale mwanjira imeneyo? Ndithudi, wopambana amene inu mungawapatse iwo! Inde, bwana. Chotero ngati munthu wathupi amaganiza zimenezo, inu mukuganiza kuti Mulungu amaganiza chiyani za ana Ake? Wopambana amene Iye angamupeze.

¹⁵⁶ Chotero, iye amafuna munthu amene ati adzakhale woonamtima. Tsopano, iye safuna munthu. . .amafuna munthuyo aziti, “Tsopano, taonani, ine—ine. . .Juniyo, iwe uzingochita zirizonse zimene iwe ukufuna, wokondedwa.” “Oh, inde, bambo, uh-huh, iye zikumuyendera bwino, iye ndi

mnyamata wabwino.” Kumusisita pang’ono pa nsana wake ndi kusasa chipewa chake. Ayi, ayi. Munthu ameneyo akhoza kuchotsedwa ntchito nthawi yomweyo. Ndithudi. Iye amafuna munthu amene angakhale woona. Ngati mnyamata ameneyo akuchita bwino, kumuuza iye. Ngati iye sakutero, kumuuza iye chimene chikulakwika.

¹⁵⁷ Ndipo ngati bambo wa padziko lapansi amaganiza zimenezo. . . Inu simungafune kuti munthu azikhala woona mtima ndi inu, mphunzitsi wa sukulu kukhala woonamtima za ana anu? Ndithudi. Chabwino, inu mukuganiza kuti Mulungu amaganiza chiyani? Ndipo Iye amadziwa; ife sitimadziwa, Iye amadziwa. Ife ndi amalire, ife sitimadziwa. Koma Iye ndi wopanda malire ndipo amadziwa.

¹⁵⁸ Chotero, inu mukudziwa chimene Atate anachita? Iwo sanati, “Ine ndipeza papa woti aziyang’anira ana Anga.” Komanso Iye sanati, “Ine ndipeza a—bishopu.” Ayi, ayi. Iye sanachite zimenezo, chifukwa Iye ankadziwa kuti papa akhoza kulakwitsa, chimodzimodzinso bishopu. Mukuona? Iye sanati nkomwe, “Ine ndipeza woyang’anira wamkulu kuti aziyang’anira mipingo Yanga.” Ayi, ayi.

¹⁵⁹ Iye anawupeza Mzimu Woyera. Umenewo unali Mphunzitsi Wake, uh-huh, kuti uzilera ana Ake. Chabwino. Ndiye inu mungadziwe bwanji kuti Mzimu Woyera ukudziwa izi? Iye amayankhula kudzera mu milomo ya munthu. Inu mungadziwe bwanji ndiye kuti Iye akunena Choonadi? Pamene inu muwona Mzimu Woyera ukuyankhula kudzera mmilomo imene ikunena Choonadi ndendende nthawi iliyonse, kuneneratu ndipo nkumadzachitika mwangwiro basi, monga Samuele ananenera, ndiye inu mudziwa kuti icho ndi Choonadi. Izo zikubwera molondola. Chifukwa Mulungu anati, “Ngati iye ayankhula ndipo zimene iye wanenazo osachitika, musamumvere iye, chifukwa Ine sindiri ndi iye. Koma ngati iye atero, chabwino, ndiye mumvereni iye, chifukwa Ine ndiri ndi iye.” Mukuona? Ndi zimenezotu. Umo ndi mmene Iye amachitira.

¹⁶⁰ Tsopano, kenako Iye akupita kuseri. Tsopano, inu mukuganiza kuti Mphunzitsi ameneyo akanena chiyani Iye akapita mmwamba kwa Atate? Ndikuti, “Anu—ana anu akuchita moipa. Ine ndikukuuzani Inu, mnyamata Wanu uja, iye, hum, iye ndi chigawenga. Iye ndi woyendayenda, ine sindinayambe ndawonapo munthu woteroyo! Mai, Inu mukudziwa zimene iye amachita? Ndi mtsikana Wanu uja! Oh, psyii, ine sindikudziwa kuti Inu muchita naye chiyani iye. Hmm. Chabwino, Inu mukudziwa chiyani? Iye akumawoneka chimodzimodzi ngati iye. . . Iye amangozipentapenta paliponse monga atsikana ena awo uko. Mfilisiti. Inde, Bwana, iye amafuna kuti azichita basi monga mmene iwo akumachitira.”

“Mwana Wanga wamkazi?”

161 “Inde, mwana Wanu wamkazi.” Izo ndi zimene Mzimu Woyera umanena za mpingo lero. Nzosadabwitsa kuti ife timalephera kuti tizikhala ndi chitsitsimutso. Mukuona? Tsopano, izo nzoona.

“Nanga bwanji mwana Wanu wamwamuna? Huh? Chinthu chomwecho.”

“Chiyani?”

162 “Chabwino, Inu mukudziwa Inu nthawizonse mumanena kuti nkhoa zimenezo zizidya mu msipu uwo kumtunda uko pa Chakudya cha nkhoa kumtunda uko. Eya, Inu mukudziwa chimene iye anachita? Iye wazithamangitsira izo kumusi uko ku mulu wa thengo umenewo. Amangozitengera izo kumusi uko ndipo amakaziponyera izo zonse mu mtsinje umenewo, ndipo amakazisiya izo kuti zigone pa mulu wa thengo umenewo, kumadya nsondozi wakale uwo, ndipo izo zikumvetsa chisoni kwambiri izo zikulephera kuti zichoke kumeneko.” Amenewo ndi mabishopu, azibusa amene amakana Mphamvu yake. “Chabwino, ine ndikukuuzani Inu choonadi, ine sindinayambe ndawonapo gulu lotero la nkhoa zamanjenje mmoyo Mwanga.” Iye samazikonda izo. Ayi. “Ndipo Inu mukudziwa chiyani? Ng’ombe zimenezo kumtunda kuno, Inu mukudziwa Inu—Inu munawauza iwo kuti azizidyetsa zijazi—alfalfa uja kumtunda uko, Inu mukudziwa, kuti izo zizinepa?”

“Eya.”

“Inu mukudziwa chimene iye akuzipatsa izo?”

“Ayi.”

163 “Thengo lakale lobaya lija. Eya. Iye akuwapangitsa iwo kuti azijowina mabungwe ndi chirichonse. Inu simunayambe mwawonapo zofanana zake mmoyo Wanu. Inu simunayambe mwawonapo zoterozo mmoyo Wanu wonse. Inu mukudziwa zimene iye akuchita? Akumapita kunja uko kumakasuta chindudu chachikulu, kubwerera mmbuyo. Iye ali ndi mkazi wake limodzi ndi iye, iye akumavala zazifupi chimodzimodzi monga Afilisiti akuchitira kunja uko. Eya.” Umenewo ndi mtundu wa uthenga umene Mzimu Woyera ukuyenera kutenga wokhudza mpingo lero. Tsopano, inu mukuganiza chiyani za zimenezo?

164 Kumeneko ndi kukhazikitsidwa. Chimene Iye... Iye anachita chiyani? Iye anatikonzera ife—ife ku kukhazikitsidwa. Iye anatipatsa ife Mzimu Woyera; koma, dikirani miniti, kukhazikitsidwa, izo ndi zimene ife tikuzikamba. Kukhazikitsidwa!

165 “Chabwino, inu mukudziwa zimene iye amachita? Abishopu anabwera tsiku lina, ndipo anadzamuuza. Iye anali akuchititsa msonkhano waung’ono wamachiritso kumusi uko, ndipo

abishopu anabwera. Munthu wina, m'bale anabwera ndipo amapempherera odwala. Ndipo iye anati, 'Iwe usiye zimenezo!'

“Oh, oh, inde, abambo bishopu, ine ndichita zimenezo.’

“Iwe usamagwirizane nazo.’

“Oh, ayi, ayi, abambo bishopu, ndithudi ayi.’

¹⁶⁶ “Ndipo apa Ine ndinabwera ndi kudzamuuzwa iye Choonadi kuchokera mu Mawu Anu omwe. Mwaona, ndi Ichi apa. Ine ndinawerenga malamulo Anu kwa iye ndendende zoti achite, ndipo iye sanamvetsere kwa izo. Iye anati, ‘Oh, zimenezo zinali za m’badwo wina, mwana wina nthawi ina yake. Zimenezo samatanthauza ine.’” Ndi zimenezotu. Izo, tsopano icho ndi Choonadi, mzunga. Tsopano inu simukuwona pamene mpingo umaphonyera kuikidwa pamalo ake, nchifukwa chiyani ife tiribe chitsitsimutso, nchifukwa chiyani ife zinthu sizikutiyendera? Pamenepo ndi pamene izo ziri.

¹⁶⁷ Yoswa akuti, “Gadi, ine ndikufuna kuti iwe...pomwe apa pali malo ako mogwirizana ndi chojambulidwa, malo ako ndi awa, pomwe apa. Iwe ukhale apa, Gadi, ndipo uzikhala apa. Benjamin, iwe upite kumusi kuno. Ndipo tsopano inu nonse mukakhale kutali ndi malire a Afilisiti.” Ndipo Yoswa akubwerera, apa iwo ali paliponse mwa Afilisiti, akukhala ndi maphwando aakulu akale, basi kumangovina monga choncho, ndipo akazi onse atazipenta, ndipo kumavina pamenepo ndi kumakhala ndi nthawi yopambana. Ndipo Yoswa akukanda mutu wake, ndikuti, “Tsopano chiyani?” Tsopano ndizo ndendende basi zimene zikuchitika; osati onse, zikomo Mulungu, osati onse, koma ambiri zedi. Chabwino.

¹⁶⁸ Tsopano chimachitika ndi chiyani ndiye? Izo ndi zimene zimachitika. Kodi inu simukuganiza kuti Munthu ameneyo, Mzimu Woyera, amachita manyazi pamaso pa Atate pamene Iye ayenera kuti akanene zimenezo? Oh, mai! “Ine—ine—ine ndinamuuzwa iye, koma iye—iye—iye samvera kwa Iwo. Ine ndinamuuzwa iye zimenezo, ndipo ndinamulola iye awerenge pomwe apo mu Bukhu. Ine ndinali—ine ndinali ndi mlaliki wamng’ono anadzabwera ndipo anadzamuwonetsa iye kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo Inu mukudziwa chiyani? Iye anamulola mmodzi wa iwo—anamulola mmodzi wa oweta mbuzi akale awo abwere kuno ndi kudzamuuzwa iye kuti izo zinali za m’badwo wina. Mukuona? Ndipo iye amanunkha moyipa kwambiri nthawi imene iye amadzafika uko, ndi fungo la mbuzi, Inu mukudziwa, ndudu, ndipo Inu mukudziwa, ndi zina zotero, amanunkha moyipa kwambiri pamene iye amadzafika kuno. Mukuona? Koma Ine ndikukuuzani Inu, woweta mbuzi ameneyo anali ndi mamendulo ambiri ataididwa pa iye, pakuti, Ine ndikukuuzani Inu, ngati Inu mungalembe dzina lake pa pepala, ilo lingatenge (mbiri yamoyo wake) zingatenge theka la mkwamba kuti mauidindo

ake akwanirepo. Inde, Bwana, iwo ndithudi amamukonda iye kumeneko mu dziko limenelo, koma, ine ndikukuuzani Inu, iye ndithudi samadziwa kuzidyetsa nkhosa. Ndicho chinthu chimodzi cha izo. Iye basi samandimvera Ine,” umatero Mzimu Woyera. “Ine ndinayesera kumuuzza iye kuti Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, koma iye—iye basi amalephera kuchita zimenezo. Iye ndi wamantha wamkulu amene Ine ndinayamba ndamuwonapo mmoyo Wangwa. Eya. Ndipo mpingo wamupanga iye kukhala woyang’anira, bishopu, zina zotero, anthu onse akumumvetsera iye. Ndiyeno Inu mukudziwa chiyani? Iwo atenga zijazi. . . iwo ali ndi chinthu chaching’ono chakale kumusi uko amachitcha ‘televizioni.’ Iwe ukayatsa chinthu chakale chaching’ono monga chimenecho, ndipo—ndipo akazi amenewo amabwerapo ndi kumatengeka nazo, mitundu yonse ya zovala zatheka. Ndipo, Inu mukudziwa, ambiri a ana Anu aakazi ndi ga- . . .”

“Oh, ndithudi ayi!” Mukuona?

¹⁶⁹ Akuti, “Inde, iwo ali. Inde, iwo akuchita zimenezo. Hum. Ena a iwo akulirira chitsitsimutso, Atate, ena a iwo ndithudi akuchifuna icho. Ena a iwo ndithudi akuyenda pa mzere, ena a iwo akuyima moona basi pa Mawu amenewo monga iwo angakhalire. Ena, ine sindikudziwa choti ndingachite, iwo—iwo ali kutali uko. Inu mukudziwa zimene ena a iwo akuchita? Akumawasereula iwo, kumati, ‘Iwo angokhala gulu la obalalika.’”

“Chabwino, zimenezo zikumandipangitsa Ine kumverera moyipa kwambiri.”

¹⁷⁰ Koma tsopano tiyeni tisinthe chithunzicho. Tsopano Atate, mwana Wake ndi mnyamata wabwino. Atate ake apo—nthawi yonse, apa pali Mphunzitsi, Mzimu Woyera. Njira imene Mzimu Woyera, Iye akati, “Ine ndiyenda,” Mphunzitsiyo anati, “Ine . . .”

¹⁷¹ Mwanayo amati, “Ine ndiyenda ndi Inu. Ine ndipita ndi Inu.”

“Oh, phirilo latalika kwambiri, mwana.”

¹⁷² “Ine ndipita nanube Inu. Ine ndiri ndi chidaliro mwa Inu. Ngati ine ndikayamba kutopa, Iye akakweza dzanja langa mmwamba ndipo akandigwirabe ine.”

“Koma kuli mikango pa phiri limenelo!”

¹⁷³ “Ziribe kanthu bola ngati Inu muli pafupi, sizikupanga kusiyana kulikonse. Ine ndizikayenda limodzi ndi Inu.

“Ndi povuta pamwamba pamenepo, miyala yake ndi yoterera.”

¹⁷⁴ “Ine sindikusamala, bola ngati Inu mukundigwira dzanja langa, ine ndizikayenda ndi Inu. Ine ndizikayenda ndi Inu.”

“Oh, inu mukudziwa chiyani? Abambo ako anakonda kuchita zimenezo, mwaona. Izo ndi zabwino. Inde, bwana.”

¹⁷⁵ Kukwera pamwamba pa phiri pamenepo. “Oh,” Iye anati, “Inu mukudziwa chiyani, Atate? Mwana Wanu ali ngati chidutswa chochokera pa chipika chakale. Iye ndithudi ali, ndendende ngati Inu. Mawu aliwonse amene Inu munena, iye amati ‘ameni’ kwa Iwo. Ine—ine ndinamupangitsa iye kuti atsegule mu Baibulo tsiku lina, ndipo Ilo linati, ‘Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.’ Inu mukudziwa chimene iye ananena? Iye anafuula ndipo anaponyera manja ake mmwamba, ndipo anati, ‘Aleluya! Ameni!’ Oh! Ndipo Inu mukudziwa Ilo linanena apa, mu—mu Mawu Anu, Inu mukudziwa, pamene Inu munati, ‘Ntchito, iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iyenso adzazichita?’”

¹⁷⁶ “Eya, Ine ndikukumbukira ndikulemba Zimenezo kwa mwana Wanga. Eya, ine ndikukumbukira ndikulemba Zimenezo.”

¹⁷⁷ “Oh, pamene iye anawona zimenezo, iye anangofuula ndipo analumpha chokwera ndi chotsika, anafuula, ‘Aleluya, Ambuye. Chotsani chidziko chonse mwa ine. Mundipange ine ndikhale monga Iwo!’ Inde, Bwana. Ndi zinthu zonse izo zimene iye anachita!”

¹⁷⁸ “Oh,” Atate anatero, “Ndine—ndine wokondwa chifukwa cha mwana ameneyo. Ameneyo ndi mwana wabwino. Chabwino. Umuyang’anire iye kwa zaka zingapo, uwone momwe iye—uwone momwe iye akuchitira, ndipo mmene iye akupitira patsogolo.” Patapita kanthawi zaka zinadutsa. “Iye akuchita bwanji?”

¹⁷⁹ “Oh, mai, komanso iye akukula mu chisomo! Oh, mai! Iye ali basi. . .Iye akumasema mitengo. Ine ndikukuuzani Inu, iye—iye ndithudi. . .Bwanji, iye amazitenga nkhosa zimenezo, akumakhoza kuzisamalira izo basi—basi monga momwe Inu mumachitira. Iye samazipatsa konse izo udzu wa mmadzi. Iye samazipatsa konse izo udzu wa maluwa. Pamene izo zibwera pamenepo, ndikuti ‘ife tikufuna tijowine tchalitchi’; iye amati, ‘Tsekani kamwa zanu, inu simukusowa zimenezo! Ayi, bwana. Ndi ichi chimene inu mukuchisowa, ‘Lapani ndipo mubatizidwe, aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu. Inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.’” Inde, Bwana, ndi zimenezo zimene iye amanena.”

“Oh, kodi iye amanenadi zimenezo?”

“Inde, Bwana, ndithudi iye amatero.”

“Chabwino, basi ndi momwe Ine ndinalembera Izo.”

“Ndi momwemo basi mmene iye amanenera Izo.”

“Hmm!” Inde, Bwana.

180 “Ena a iwo amati, ‘Dikirirani inu mu mzinda wa Yerusalemu mpaka inu mutadzazidwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba. Mzimu Woyera ukabwera pa inu, inu mudzakhala mboni za Ine mu Yerusalemu, Yudea ndi Samaria, ndi madera akutali a dziko lapansi.’ Pamene iye anawerenga zimenezo, anafuula, ‘Aleluya, izo ndi zimene inu mukuzisowa!’ Inu mukudziwa zimene iye amachita? Iye amangowatenga iwo pamenepo mpaka iwo atamvetsa Izo, ndizo zonse, amangokhala ndi iwo.

181 “Ndipo ngati iwo ayamba kukangana, iye amati, ‘Wuupu, wuupu, wuupu, dikirani miniti, dikirani miniti. Umo ndi mmene mbuzi zimachitira, osati nkhoa. Mukuona? Mukuona?’ Oh, nthawizina iwo amakwiya naye pang’ono, koma iye amakhala ngati amawasisita iwo pa nsana pang’ono chabe, amati, ‘Dikirani miniti, shi-shi, shi-shi, shi. Izo ziri bwino.’ Iye amadziwadi mmene angazisamalire nkhoa zimenezo. Inde, Bwana, Ine ndikukuuzani Inu.

182 “Inu mukudziwa chiyani? Ine ndinamuwona Arkibishopu *Wakuti-ndi-wakuti* akumuuzza iye kuti iye ‘sangabwere ku mzinda uno ndi kudzachititsa msonkhano.’ Koma, Inu mukudziwa, Ine ndinakhala ngati ndinamutsogolera iye, Ine ndinati, ‘Upitebe mulimonse.’ Mukuona? ‘Kachotseniko matepi awa, ndipo musawalole kuti iwo apite uko.’ Ife tinapitabe mulimonse! Tinapita mmizinda iyi kuno, tinati, ‘Chabwino, ife sititha- . . .’

183 “Ndipo Inu mukudziwa, mdierekezi anapita kumeneko, anati, ‘Ine ndikukubetchera Iwe ine ndikhoza kumuchotsa iye ku mzinda uwo.’ Ine ndinati, ‘Sungachite zimenezo. Ngati ine ndimuuza iye kuti azipita, iye apita. Ine ndikukubetchera iwe iye apita.’ ‘Ayi, ayi, ayi, ayi, ayi, ine ndimuuza iye. Ine ndipita kumeneko ndipo ndikati, “Tsopano, antchito anga onse, inu nonse musonkhane pamodzi. Inu simukufuna chirichonse cha kutengeka kwachikale uko kumusi kuno, machiritso Auzimu achikale onse awo ndi zinthu zakale za Mzimu Woyera izo. Zimenezo zinapita kale ndi atumwi zaka zapitazo. Inu mukudziwa kuti zimenezo si zabwino, kumbuyo uko.” Akuyesera kumawapatsa iwo udzu wamaluwa, chirichonse monga chomwecho. Iwo . . .

184 “Koma, Inu mukudziwa chiyani, iye anapitirirabe kumusi uko mulimonse. Anapitirira mpaka anatsikira kumusi ndipo anakayamba kuponya alfalfa, kuchokera . . . Ndipo Inu mukudziwa chiyani, nkhoa zimenezo zinayamba kudya, izo zayamba kunenepa mmene izo zingathere. Inde, Bwana. Pamene iwo akukhala ndi machiritso ndi misonkhano ndi, Inu mukudziwa, ambiri a achinyamata awo ayambapo. Bwanji, iwo awona kuti akadya mulu wa msipu wonga wa alfalfa uja. Inu mukudziwa chimene iwo achita nawo iwo? Iwo unali wabwino kwambiri mpaka iwo anathamangira nawo kwa oyandikana nawo, anati, ‘Lawani Uwu! Lawani Uwu! Lawani

Uwu!’ Mwaona, chikhalidwe cha pamalo kumeneko chimakoma chimodzimidzi basi ngati ichi komwe kuno. Ndi Ichi pomwe apa. Ndi Ichi pomwe apa, mwaona. ‘Mungolapa, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu, mwaona, inu mulandira Mzimu Woyera. Iwo ndi wa aliyense amene akuufuna, muloleni iye abwere, muloleni iye abwere kuno kuti adzawone chimene Baibulo linanena.’ Mukuona? Ndipo iwo akungokhala ndi nthawi yopambana kumusi uko.”

¹⁸⁵ “Oh, ameneyo ndi mwana Wanga! Ameneyo ndi mnyamata Wanga. Chabwino, Iwe ukuganiza kuti iye wakhwima bwino?”

¹⁸⁶ “Inde. Ndithudi ndikutero,” unatero Mzimu Woyera. “Ine ndamuyesa iye. Mnyamata, ine ndinamuyesa iye mwanjira *iyi*, ndinamuyesa iye mwanjira *iyi*. Ine ndamuponyera iye pansi, kudwala, ine ndinamuika iye pansi. Ine ndinamuponda iye, Ine ndinamusiya mdierekezi kuti achite chirichonse kwa iye chimene akanatha kuchichita, iye anadzadzukanso kachiwiri. Iye anabwera chimodzimidzi basi. Mwaona, anabwereranso kachiwiri. Ine ndinamudwalitsa iye. Ine ndinachita *ichi*. Ine ndinamuponyera iye mchipatala. Ine ndinamutengera iye kunja kuno Ine ndinachita *ichi*, Ine ndinachita *icho*. Ine ndinapangitsa mkazi wake kuti adane naye iye, Ine ndinapangitsa oyandikana naye kuti amutsutse iye, Ine ndinapangitsa chirichonse. Zimenezo sizinapange kusiyana kulikonse. Anati, ‘Ngakhale Iye atandipha ine, komabe ine ndidzamudalira Iye.’ Ine ndinapha banja lake. Ine ndinatenga *ichi*, ine ndinachita *ichi*, ine ndinachita zonse *izi*, ine ndinachita *ichi*, *icho*, *chinacho*. Komabe iye anayima moongoka, ‘Ngakhale Iye atandipha ine, komabe ine ndidzamutumikira Iye! Iye ndi wanga!’”

¹⁸⁷ “Oh! Chabwino, ine ndikukhulupirira Iye tikuyenera timuitanire iye kwinakwake kumalo aang’ono apadera ndipo tikakhale ndi kukhazikitsidwa.”

¹⁸⁸ Tsopano, pamene bambo, mu Chipangano Chakale, akamva kuti mwana wawo wafika pa usinkhu, ndipo anali woti wafika poti akhazikitsidwe. Ku! Iwo amabadwa ali mwana, koma, pamene iwo ali mwana wa mwamuna pamenepo. Komano iwo sikuti azingokhala mwana chabe, mwana wa mwamuna wawamba, kufikira iwo akhwime ndi kumawonetsera chimene iwo ali. Kenako, iye amamuitanira iye kunja uko ndiye.

¹⁸⁹ Tsopano ndife pano, mpingo. Kodi inu mwakonzeka? Tsopano tachedwa pang’ono, aliyense lumani chala chanu, mutsine solo yanu, ndipo mukhodoble mtima wanu, basi kwa miniti. Mukuona? Tsopano ife tiwukhazika mpingo. Tsopano pamene mpingo ufika pamalo amenewo, Iye amati, “Manasse, iwe ndi wa apa. Efremu, iwe apo.”

¹⁹⁰ Zikatero iye amamutengera iye pamalo enaake, abambowo amatero, ndipo iwo amakamukhazika iye pa malo okwera

monga chonchi, ndipo iye amakakhala ndi mwambo, ndipo iwo onse amabwera kudzazungulirapo. Ndipo iye amati, “Ine ndikufuna aliyense kuti adziwe kuti uyu ndi mwana wanga, ndipo ine ndikumukhazikitsa mwana wanga. Ndipo ine ndikufuna aliyense adziwe, kuyambira lero, kuti dzina lake . . . Ine ndikumuveka iye, chovala chapadera pa iye. Ndipo ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti dzina lake ndi chimodzimodzi pa cheke chirichonse ngati dzina langa. Iye ndi mwana wanga, ine ndikumukhazikitsa iye alowe m’banja mwanga, ngakhale iye wakhala ali mwana wanga wa mwamuna chibadwireni chake. Kuyambira pamene iye analandira Mzimu Woyera, iye wakhala ali mwana Wanga wa mwamuna. Koma tsopano ine ndikumuyika iye pa malo ake a ulamuliro. Amene iye wamuchotsa ntchito wachotsedwa ntchito, amene iye wamulemba ntchito walembedwa ntchito:

¹⁹¹ “Ndipo indetu, indetu, ine ndinena ndi inu, ngati inu mudzanena kwa mtengo uwu, ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘suntha,’ ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene inu mwanena chichitika, inu mukhoza kulandira chimene inu mwanenacho.” Mukuona? Ndi zimenezotu; ndi zimenezotu. Mukuona? “Iye ndi mwana Wanga.” Ndi angati amene amadziwa kuti kukhazikitsidwa, kuti a . . . iwo amamukhazikitsa mwana wa mwamuna iye akawatsimikizira kuti ndi . . . Aliyense amene anayamba wawerengapo Baibulo, kuikidwa pa malo kwa mwana.

¹⁹² Tsopano, Mulungu anachita chinthu chomwe chomwecho kwa Mwana Wake pamene Iye anamutengera Yesu pamwamba pa Phiri la Chiwalitsiro. Iye anamutengera Petro, Yakobo ndi Yohane pamwamba pamenepo, zimenezo ndi mboni zitatu za pa dziko lapansi. Panali Yesu, Mose ndi Eliya, ndi Mulungu, pamwamba pa phiri. Pamenepo iwo anaima pamenepo pa phiri. Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anayang’ana, ndipo Yesu anapatsidwa ulemelero pamaso pa iwo. Nkulondola uko? Ndi angati amene akudziwa kuti zimenezo ndi Lemba? Kodi Iye anachita chiyani? Iye—Iye anamuveka Iye mwinjiro wa chisavundi. Ndipo iye anati, “Chovala chake chinwala ngati dzuwa.” Nkulondola uko? Ndipo mtambo unawaphimba iwo. Ndipo Petro ndi Yohane ndi iwo, anagwa pa nkhope zawo. Ndipo iwo anayang’ana, ndipo pamenepo panaima Mose ndi Eliya, akuyankhula ndi Iye. Ndipo Mose anali atafa, ndipo anaikidwa mmunda osadziwika kwa zaka eyiti handiredi. Ndipo Eliya anakwera pa galeta kupita Kumwamba, zaka faifi handiredi izo zisanachitike. Psyi! Koma iwo anali akadali kumeneko! Pamenepo iwo anali kuyankhula ndi Iye. Mwaona, Iye anamutengera Yesu pamwamba kuti akawawone iwo, kuti akawone chimene izo zonse chinali, kukawona kumeneko, kukamuwonetsa Iye zinthu izi. Ndipo iwo anayankhulana ndi Iye, anali ndi zokambirana ndi Iye.

¹⁹³ Kenako mwamsanga pamene Petro anayang'ananso mmbuyo ndipo ulemelero unali utachoka pa Yesu, iwo anamuwona Yesu Yekha, ndipo Liwu linabwera kuchokera mu mtambo uwo, ndipo linati, "Uyu ndi Mwana Wanga wokonededwa, mumvereni inu Iye! Dzina Lake ndi chimodzimidzi basi ngati Langa tsopano. Mvereni inu Iye!" Ndi zimenezotu, wakhazikitsidwa, kapena ana oyikidwa pamalo.

¹⁹⁴ Tsopano, pamene ndi pamene Mulungu akuyesetsa kuti awutengere mpingo wa Chipentekoste mu Bukhu la Aefeso. Mukuona? Kodi inu, kodi inu mukumvetsa? Ife tikuyenera kuti titseke chifukwa kukuyamba kuda, mwaona, ana akuyamba kusinza. Ndipo ine ndimafuna kuti ndifike apa pa ndime iyi pomwe apa, koma ine sindingachite zimenezo, mpaka a—ndime ya 13, mwaona, gawo lotsiriza, "kusindikizidwa ndi Mzimu Woyera wa lonjezo." Ife tidzatenga zimenezo Lamlungu, mwaona. Onani. Tsopano, motani, nchiyani chimene chimatilowetsa ife mkati, ndi mmene ife timasungidwira ndi Ichi.

¹⁹⁵ Koma tsopano "kuikidwa pamalo," inu mumatani? Inu poyamba mumabadwira mu Ufumu mwa Mzimu Woyera. Ndi angati amadziwa zimenezo? Chabwino. Chotsatira, inu munakonzedweratu kwa chiyani? Kukukhazikitsidwa. Ndi chiyani chimenecho? Inu munakonzedweratu kudzaikidwa pamalo.

¹⁹⁶ Oh, Mlongo Scott, ine ndikukhulupirira ndi inuyo, mwakhala apa. Kodi si inu amene munabwera kunyumba lero? Chiphunzitso chikuzungulira kwinakwake mdziko, kuzungulira madera osiyanasiyana a mdziko, ine ndamvapo za izo, zochuluka, kuti Yesu ali pano pa dziko lapansi, akuyendayenda mthupi, Iye amabwera ndipo amadzachita *izi*. Limenelo ndi bodza! Mzimu Woyera Wake uli pano, ndipo Iye akuyesetsa kuti awukhazikitse Mpingo Wake, kuti awuyike Mpingo Wake mu dongosolo, awuyike iwo mu Dziko lolonjezedwa, kuti iwo akakhoze kulowa . . . kuti adani onse apitikitsidwe panja.

¹⁹⁷ Manasse sakutenga dziko lake. Ine sindingakhale ndi msonkhano wamachiritso pamene theka la . . . pamene a . . . Ine ndimapita uko ndi kukalalikira ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo a—abale autatu amati, "Oh, iye ndi wa Yesu Yekha wakale." Ndipo ine sindingapite kuno ndi kukakhala ndi machiritso Auzimu pamene theka la iwo amati, "Machiritso Auzimu ndi abwino," ndipo ambiri a iwo nkumasangalala ndi zozizwitsa za Ambuye ndipo kumati, "Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti M'bale Branham ndi mneneri, koma ndiloleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Nthawi yonse pamene Mzimu uli pa iye, ndipo akuzindikira za mumtima, iye amakhala wantchito wa Ambuye. Koma Chiphunzitso chake ndi chovunda, Icho si chabwino." Ndi ndani amene anayamba wamvapo zovunda zimenezo? Icho

ndi cha Mulungu kapena si cha Mulungu. Uko nkulondola. Izo zonse ndi za Mulungu kapena palibepo za Mulungu. Umo ndi mmene izo zimakhallira. Koma inu mungakhale nazo bwanji? Manasse akulephera kusunga malo ake, Efremu akulephera kusunga malo ake, Gadi akulephera kusunga malo ake, Benjamini akulephera kusunga malo ake, iwo onse akuthamangathamanga kunja kuno ndi Afilisiti, ndipo onse angosokonezeka. Ife tiikidwa bwanji pamalo? Koma ife tinabadwa mwa Mzimu Woyera, tonse a ife. Nkulondola uko? Ife tinabadwira ku chiyani? Kukonzedweratu... Kenako titatha kubadwa, ife timakonzedweratu ku kukhazikitsidwa, kuti tidzaikidwe mu Thupi la Khristu. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

¹⁹⁸ Kodi Thupi la Khristu ndi chiyani? Ena ndi atumwi, ena ndi aneneri, ena ndi aphunzitsi, ena ndi avangeri, ndipo ena ndi abusa. Nkulondola uko? Ife tinaitanidwirako. Ena ali ndi mphatso za malirime, kutanthauzira kwa lirime, nzeru, chidziwitso, zozizwitsa, kuchita kwa zozizwitsa, mphatso zonse zosiyanasiyana izi. Ndipo tsopano kodi iwo anachita chiyani? Iwo anachita zimenezo pang'ono pokha. Chiyani? Azilola izo zibalalike monga ngati ine sindikudziwa chiyani. Wina amadzuka, amayankhula mmalirime, ndipo wina amapitirira, kumayankhula, “Bluruu, bluruu, bluruu, bluruu, blii” Uh-huh. Mlaliki uyu akhala akulalikira, akuyitanira paguwa, ndipo winawake nkudzadzuka, kudzayankhula mmalirime ndi “Aleluya, ulemelero kwa Mulungu.” Ngati a... ngati mlalikiyo apezeka kuti akupitirira ndi uthenga wake, pokhala kuti wadzozedwa, ndiye anthu amati, “wobwerera mmbuyo wakale.” Mwaona, ndi chifukwa chakuti iwo sanaphunzitsidwe.

¹⁹⁹ Baibulo linati mzimu wa aneneri umamumvera mneneri. Mulungu si woyambitsa chisokonezo. Pamene ine ndiima pano, kapena mtumiki akakhala pano pansu pa kudzoza kwa Mulungu. Ziribe kanthu kuti ndi mochuluka bwanji mmene inu mungafunire kuyankhula ndi malirime, inu mukhale bata kufikira Mulungu atamaliza apa. Kenako ngati inu muyankhula ndi malirime, izo sizingangokhala kubwereza kwa Lemba, chifukwa Mulungu anati musamagwiritse ntchito kubwereza kwachabe. Koma iwo uzikhala uthenga wolunjika wopita kwa winawake. Mudzandifunse ine nthawiina, mudzaike chala chanu pa wina nthawi ina amene Mzimu Woyera unayambapo, pansu pa kuzindikira za mumtima, unamuuzapo winawake, mongobwereza bwereza Lemba. Iwo unawauza iwo chinachake chimene chinali cholakwika ndi iwowo ndi chinachake chimene iwo anali atachita, ndi chinachake chimene iwo akuyenera kuchita kapena chinachake chimayenera kuti chichitike, kapena chinachake monga chomwecho. Nkulondola uko?

²⁰⁰ Chimodzimodzinso ndi kuyankhula mmalirime ndi kutanthauzira! Ngati alipo mmodzi mu mpingo amene

amayankhula ndi malirime, ndipo wina amatanthauzira iwo, mulole iwo azinena izi. Kumulola M'bale Neville azidzuka ndi kuyankhula ndi malirime, ndipo m'bale uyu apa nkupereka kutanthauzira, kuti, "Mumuuze munthu uyu apa kuti dzulo iye anapita kunja kuno ndipo anakachita chinachake chimene iye samayenera kuti achite. Tsopano adokotala amuuza iye lero kuti ali ndi khansa. Apite akakonze chinthu chimenecho, adzabwerere kuno ndipo adzakonze kwa Mulungu."

Munthuyo nkuti, "Zoonadi, izo ndi zoonu." Ndiye kuti Mulungu ali ndi inu.

²⁰¹ Koma ife tikuchita bwanji izo mwanjira iyi? Mukuona? Ndizo basi, "Blimpu, bluruu, bluruu, bluruu." Basi mwachisawawa, mwanjira iliyonse, opanda kuyikidwa pamalo nkomwe. Tsopano ndizo... Mwaona, Aefeso, akuyesetsa... Mwaona, iwo akuphonya zimenezo. Mukuona mmene iwo amaphonyera izo? Ife tinakonzedweratu ku kukhazikitsidwa kwa ana! Tsopano ndi angati amene akumvetsa chimene ine ndikutanthauza, kwezani mmwamba dzanja lanu. Kukhazikitsidwa! Ife tinabadwa mu Mzimu wa Mulungu, ndithudi, tinalandira Mzimu Woyera, ndipo timalira, "Abba, Atate! Aleluya! Ulemelero kwa Mulungu!" Ndife, uko nkulondola, ndife ana, koma ife timalephera kupita kulikonse. Ife timalephera kumukwapula Mfilisiti.

²⁰² Tamuwonani Billy Graham atayima uko. Ndi wa Chimuhamadi uja akuti, "Tsimikizira Izo."

²⁰³ Tamuwonani Jack Coe atayima kumusi uko. Ndipo wachikunja uja, mpingo wa Khristu uja kumagwirana chanza ndi wachikunja kunja uko, ndi kumathandizirapo. Amayenera kukhala Mkhristu, ndipo nkumagwirana chanza ndi mdierekezi monga Joe Lewis, ndi woganiza mwaufulu, ndipo ngakhale kumunyoza Mulungu ndipo anati "kulibeko chinthu choterocho ngati Mulungu, mulimonse, kuyamba ndi kuyamba," ndi zinthu monga zimenezo. Ndipo mpingo umene umadzitcha wokha mpingo wa Khristu, kumagwirana chanza ndi iye, ndipo nkumatenga mbali momutsutsa M'bale Jack Coe. Ife tingachite bwanji chirichonse? Ndipo Achipentekoste, ambiri a iwo, kumamutsutsa iye; pamene, mlaliki aliyense mu dziko lathu akuyenera kuyima phazi ndi phazi ndi iye, ndipo anati, "Mulungu, tsitsirani pansu Mphamvu Yanu." Mwaona, ndi zimenezotu ife, pamene izo sizingaikidwe pamalo.

²⁰⁴ Efremu sakufuna kukhala. Wina wa iwo akupita kuno, ife tikumupeza Manasse akupita kuno, akuti, "Oh, mai, Ambuye andipatsa ine munda wabwino wachimanga!" Kenako apa akubwera kuno, Gadi, anati, "Chabwino, tsopano, dikira miniti. Ine ndikuyenera ndizilima tirigu, koma ine ndipeza chimanga aponso. Aleluya!" Inu mukuona? Inu mulibe kanthu kochita ndi chimanga; kapezeni tirigu, tirigu ndi mbali yanu yoti muzilima.

Inu simukuyenera kuweta nkhosa pamene inu mukuyenera kuweta ng'ombe. Mulungu akufuna kuwuyika mpingo pamalo. Koma mmodzi aliyense wa iwo akufuna kuchita chinthu chofanana. "Aleluya!" Ndipo inu simungawauze iwo chinthu cha izo. Ayi, ayi. Iwo akadali nachobe chikhalidwe cha mbuzi icho, "Batti, batti, batti, batti, batti, batti, batti." Mwaona, inu simungawauze iwo. Uko nkulondola. Tsopano, kodi izo sizooka? Ndipo inu simungawuike mpingo pamalo. Mukuona?

²⁰⁵ Mpingo ukuyenera kukonzedweratu ku kukhazikitsidwa kwa ana, kumene munthu... Mulungu akhoza kumutenga munthu ndi kumukhazikitsa iye mu banja, ndi kumupatsa iye chinachake. Chimenecho, poyamba, muchiyese icho ndi kuwona ngati chiri chondola. Baibulo linati uyeseni mzimu. Munthu uyu akudzinenera chinthu chinachake, chiyeseni icho ndipo muwone ngati chiri cholondola. Ngati icho chiri cholondola, yendani nacho icho. Kenako munene, "Ambuye, titumizireni ife chinachakenso." Zisunthanibe, mwaona, basi zisunthanibe mpaka munthu aliyense atatenga malo ake. Mukatero inu muwuwona mpingo wa Mulungu ukuyamba kutenga malo ake. Pamenepo ndi pamene Afilisiti atayambe kubwerera mmbuyo. Akabudula achokapo, tsitsi likula mpaka pansu, nkhoze zidzatsukidwa; ndudu zidzakhala zikusowa. Uko nkulondola. Pamene Mpingo udzayamba kubwera mu Mphamvu yake yaikulu, pamene ife tidzakhale ndi Ananiya ndi Safira, ndi apang'ono a iwo. Inde, bwana. Inu mudzawona pamene Mpingo woyera umenewo udzaima pamodzi mu Mphamvu Yake, ukuikidwa pamalo ake ngati ana a Mulungu, akukhazikitsidwa kulowa mu banja la Mulungu, Mpingo wamphamvu utayima pamenepo mu ulemelero wake. Oh, icho ndi chimene Iye akudzera.

²⁰⁶ Mukuona mmene ife tapitira kutali, abale? Inu mumalephera ngakhale kubwera pamodzi pa Lemba. Ndipo munthu aliyense, munthu aliyense amene sangawone ubatizo wa mmadzi mu Baibulo, mu Dzina la Yesu Khristu, iye mwina ndi wakhungu kapena chinachake ndi cholakwika mu ubongo. Uko nkulondola. Ndipo apo ndi pamene pamakhala ndewu yaikulu.

²⁰⁷ Ine—ine ndimuuzwa munthu aliyense yemwe angandibweretsere ine Lemba lililonse pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina lina lililonse kupatula Dzina la Yesu Khristu, mu mpingo watsopano. Kapena, ngati iye anabatizidwa mwanjira ina iliyonse, iye ankayenera kuti abatizidwenso mu Dzina la Yesu Khristu, kuti alandire Mzimu Woyera. Inu mubwere mudzandisonyeze ine. Palibepo zoterozo. Palibepo kutuma koteroko. Pamene Yesu ananena apo, "Chotero inu pitani, kaphunzitseni mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Atate, Mwana, ngakhalenso Mzimu Woyera, palibepo limene liri dzina, palibe la iwo. Petro anapitoloka, masiku teni mtsogolo, anati, "Lapani,

ndipo mubatizidwe, aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu, ku chikhulukukiro cha machimo.” Ndipo paliponse mu Baibulo.

208 Ndiyeno apa ena amene anabatizidwa kumusi uko, mwanjira ina iliyonse, ndi Yohane, basi ku kulapa. Paulo anati, “Inu mukuyenera kuti mubatizidwenso. Inu mukuyenera kuti mubwere kachiwiri.”

209 “Oh, koma ife tinabatizidwa ndi mwamuna woyera, Yohane. Iye anamubatiza Yesu.”

210 “Chabwino, uwu ndi Uthenga. Uwu ndi Mzimu wa Mulungu umene wakhalapo woti uwululidwe kwa ine. Ine ndi mtumwi wa Ambuye, ndipo ngati mngelo wochokera Kumwamba abwera ndi kudzalalikira china chirichonse. . .”

211 Ndiloleni ine ndiwerenge zimenezo. Baibulo linati, “Ngati mnge- . . .” Paulo anati, “Ngati mngelo wochokera Kumwamba anena china chirichonse,” bishopu, arkibishopu, papa, woyang’anira, chirichonse chimene iye angakhale, “ngati iye alalikira china chirichonse kupatula Ichi chimene ine ndalalikira kwa inu, msiyeni iye akhale wotembeleredwa.” Palibepo ayi. . .Ife tiribe miyambo yonga imeneyo. Ayi, bwana. Inu basi. . .Palibepo chinthu ngati chimenecho. Inu, ife. . .Ndiyeno—kenako, mwaona, nchifukwa chiyani kuti anthu sakuwona zimenezo? Nchifukwa chiyani anthu akulephera—akulephera, akulephera kukhulupirira zimenezo? [Winawake mwa osonkhana akuti, ‘Anakonzedweratu’—Mkonzi]. Mukuona? Winawake wachimenya bwino icho apo, Gene. “Kukonzedweratu,” ndendende. Chifukwa chiyani? “Onse amene Atate andipatsa Ine” (chiyani?) “adzadza kwa Ine.” Ndendende motani! “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza, adzadza kwa Ine.” Vuto langa ndi chiyani, ine ndikuyesetsa kupeza apa? Ndi ife apa. Chabwino.

212 Ndiloleni ine ndingowerenga ndime iyi ndipo kenako ine ndikuuzani inu chimene Paulo, zinthu zimene. . .Uthenga womwewo umene ine ndalalikira usikuuno, ndi izi zimene Paulo ananena za kukonzedweratu, pa ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu, ubatizo wa Mzimu Woyera, dongosolo la mu mpingo, ndi zina zotero. Ndi izi zimene iye ananena.

Ine ndikudabwa (akuwauza Agalatiya awa) kuti inu mwachoka mwamsanga kwa iye amene anakuitanani inu ku. . .chisomo cha Khristu. . . (Ine ndachita manyazi kwambiri ndi inu, mwa kuyankhula kwina, kuti inu mwamulola winawake kuti alowe ndi kudzakupotozani inu kuti muchoke kwa Icho.) kupita ku uthenga wina:

Umene si wina; koma pali ena amene akukuvutitsani inu, ndipo akhoza kuletsa uthenga wa Khristu, kuletsa Uthenga weniweni wa Khristu.

213 Koma penyani. Tsopano, kumbukirani, anali Paulo amene anakakamiza munthu aliyense amene sanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, kuti abwere ndi kudzabatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu. Ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? Ndi angati akudziwa kuti anali Paulo amene anati zinsinsi izi zinabisidwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, ndipo zinaululidwa kwa iye, kuti ife tinakonzedweratu kuti tidzakhale ana, ndipo, ku kukhazikitsidwa. Anali Paulo. Onani apa zimene iye ananena.

Koma ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, akalalikira uthenga wina uliwonse kwa inu wosiyana ndi uwo umene ife tinalalikira kwa inu, msiyeni iye akhale wotembereredwa.

214 Basi osangoti, “Ine sindikugwirizana nanu inu, bambo.” Basi kungomusiya iye akhale wotembereredwa. Ndiloleni ine ndiwerenge ndime yotsatira.

Monga tinanenera mmbuyomo, chomwechonso ine ndikunena kenanso, Ngati munthu aliyense alalikira uthenga wina uliwonse kwa inu wosiyana ndi uwo umene ife talandira kale, mulole iye akhale wotembereredwa.

215 Uko nkulondola. Tsopano, m’bale, mlongo, ngati anali Mulungu tsiku lina, ndipo ine—ine ndikunena zimenezo poyembekeza kuti si mosalemekeza, chimene chinanditenga ine kuti ndikawone chaching’ono ichi...Tsopano, ine ndimatengeka; ine sindikuganiza kuti ndimatengeka, ine ndimangodalitsika mu kulalikira. Ine ndimatengeka ndipo ine ndimakusungani inu pano mpaka ine kumadziwa kuti mukusinza ndipo mwatopa. Koma, oh, ine...Ngati inu—ngati inu mukanangodziwa mmene ine ndimakufunirani inu kutsidya uko! Mukuona? Ndipo pamene ine, kamodzi ine ndikunena ichi kenanso, pamene ine...pamene Iye anati...ine ndinati, “Izo zidzatero...”

Iye anati, “Kodi iwe ungafune utawona kuti mapeto adzakhala chiyani?”

216 Ndipo ine ndinayang’ana mmbuyo ndipo ndinadziwona ndekha nditagona apo pa bedi. Ndithudi inu mwandidziwa ine utali wokwanira kuti mukhoza kudziwa kuti—kuti—kuti ine ndikukuuzani inu Choonadi. Ine ndikufuna kuti ndikufuneni inu chinachake, monga Samuele ananenera iwo asanamudzowe Saulo, kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinali choona? Nkulondola uko? Izo nthawizonse zakhala ziri zoona. Kodi ine ndinayamba ndabwerapo kumadzakupemphani ndalama kapena chirichonse ngati chimenecho? Ayi, mwaona, ine sindinateropo. Kodi ine ndinayamba ndachitapo chirichonse koma kuyesetsa mwa

kupambana kwanga kuti ndikutsogolereni inu kwa Khristu? Ndendende.

²¹⁷ Tsopano iwo akufuna azinena kuti ine ndi wowerenga maganizo, inu mukudziwa, kumvetsa zinthu mwapamwamba. Ndithudi, zinthu zimenezo zikuyenera kuwuka, Baibulo linati zidzatero. Monga Ayambule ndi Ayane anamutsutsa Mose, iwo amachita pafupifupi chinthu chomwecho chimene Mose ankachita, mpaka izo zinafika pa chiwonetsero. Uko nkulondola. Koma kumbukirani, Ayambule ndi Ayane samatha kuchiritsa. Iwo samatha kuchiritsa. Iwo amatha kubweretsa miliri, koma osati kuichotsapo iyo. Mukuona? Chabwino. Tsopano, Mulungu ndi Mchiritsi. Mawu a Mulungu amakhalabe Choonadi.

²¹⁸ Ine ndayesetsa kukhala woonamtima ndi inu. Ine ndayesetsa kukuuzani inu Choonadi. Ine ndatero—ine ndatero... kwa pafupifupi zaka sate-wani, ine ndaima pa guwa lino, kuchokapo ndi kubwerapo, kwa zaka sate-wani, ndipo tsikulina ndidzachoka kupita ku Ulemelero kutalikirana ndi guwa ili. Kumeneko anapita kale mkazanga, mwana wamkazi, bambo, mchimwene, onse anaikidwa kutsidya uko, abwenzi ofunika. Ine ndinawona mabokosi awo ndi maluwa zikuikidwa kuno. Ndipo ndikudziwa tsiku lina langa lidzakhala uko, nanenso. Tsopano, izo ndi zooni. Koma moonamtima, kuchokera mu mtima wanga wonse, ine ndikukuuzani inu ndi mtima wanga wonse, ine ndikukhulupirira ndalalikira kwa inu Uthenga woota wa Ambuye Yesu Khristu. Ine ndikukhulupirira kuti inu mukuyenera kubatizidwa, aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo nthawi iliyonse inu mungatero, izo zidzabweretsa kwa inu chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, ubwino, chifatso, chifundo, chipiriro, chikhulupiriro.

²¹⁹ Ndipo tsiku lina, chimene chinandichitikira ine mmawa umenewo, ine sindikudziwa. Ine sindinganene panobe kaya ndinali kuno mu thupi langa ndipo ndinangowona masomphenya, kapena kaya ine ndinatengedwa kuchoka kuno, kupita uko. Ine sindikudziwa, ine sindinganene. Chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa, kuti ine—ine nthawizonse ndimawopa kufa, malo aang’ono amenewo a mbola. Koma sikuti ndimawopa kuti Yesu sabwera kudzanditenga ine, tsopano, ine sindimawopa zimenezo, chifukwa ine—ine sindimawopa zimenezo; koma ngati ine ndingadzakumane nanu inu ndipo nkungokhala ka mtambo kakang’ono kakuuluka kunjira mu mpweya. Koma ine ndikuwona tsopano. Pamene ine ndinawawona anthu amenewo, iwo anali enieni. Ndipo iwo anali anthu amene nthawiina ankayanjana ndi ine kuno pa dziko lapansi, ngakhale kwa mkazi wanga woyamba. Iye sanali mkazi wanga, iye anali mlongo wanga. Iye sananditchule ine mwamuna wake, iye ananditchula ine m’bale wake

wokondedwa. Kunalibepo kugonana, kunalibe zogirigisha za mtundu umenewo, izo sizikanakhalako; iwo unali ungwiro, iwo unali ukoma, unali ungwiro.

Ine ndikudabwa, ine sindikudziwa, ine ndikudabwa: Kodi icho ndi chimene iye ankachiwona, iye asanachoke pa dziko lapansi, pamene iye anali uko mu chipatala, pamene ine ndinamuitana iye? Ndipo iye anati, “Billy, iwe wachilalikira icho, iwe wachiyankhula icho, koma,” iye anati, “iwe sukudziwa chimene icho chiri.” Iye anati, “Ine ndiribenso chikhumbo choti ndikhale.”

²²⁰ Ine ndikudabwa ngati icho ndi chimene chiri, ndi bambo waumulungu uja, woyera wokalamba F. F. Bosworth, amene anaima pa guwa ili, amene walalikira nane kuzungulira magawo osiyanasiyana a dziko. F. F. Bosworth wokalamba, nonse a inu, pafupifupi, mumamudziwa iye; waumulungu, bambo woyera wokalamba. Maora awiri asanati, chabwino, pafupifupi sabata kapena awiri iye asanasamuke, ine ndinapita kwa iye ndipo pamenepo iye anali atagona kumbuyo uko, kutali, pafupifupi usinkhu wa zaka nainte. Mikono yake yaing’ono inafikira, mutu wake waung’ono wa dazi ndi ndevu zoyera zija ziri pa nkhope yake. Ine ndinamunyamula bambo wokalamba ameneyo mmikono mwanga ndipo ine ndinafuula, “Atate anga, atate anga, magareta a Israeli ndi amuna apa kavalo ake.”

Pakuti ngati panayamba pakhalapo munthu amene anaimirira Pentekoste ndipo anali mtumwi woota, anali F. F. Bosworth, woyera, wopanda psyete, Uthenga weniweni, mwaona, anali Bosworth. Ndipo pamene ine ndinamugwira iye mmikono mwanga, ndipo ine ndinafuula, “Atate anga, atate anga, magareta a Israeli ndi amuna apa kavalo ake.”

²²¹ Iye anati, “Mwana, khala mmunda.” Anati, “Uwathamangitsire ena a achinyamata awa ku minda yakutali, ngati iwe ungate, iwo asanatenge kutengeka kuchuluka uko. Uwatengere iwo Uthenga weniweni uwo umene iwe uli nawo, mwana.” Iye anati, “Utumiki wako sunayambe apobe kwa chimene iwo udzakhalale.” Anati, “Ndiwe Branham watsopano.” Anati, “Ndiwe wamng’ono, mwana.”

Ine ndinati, “M’bale Bosworth, ine ndi wausinkhu wa zaka forte-eyiti.”

²²² Iye anati, “Iwe sunayambebe apobe.” Iye anati, “Usawalole alaliki aang’ono Achipentekoste awa kuti apite kumeneko ndi zamkhutu zochuluka, ndi kukachipatsa chiphe chinthucho, ndi kukawapangitsa onse—akazembe ndi dziko lonse kuti azitsutsa Iwo iwe usanakafike kumeneko.” Anati, “Zisunthanibe, M’bale Branham, zipitiriranibe ndi Uthenga umene iwe uli nawo.” Iye anati, “Ine—ine ndikukhulupirira kuti ndiwe mtumwi, kapena mneneri wa Ambuye Mulungu wathu.”

223 Ine ndinamuyang'ana iye, ine ndinamukumbatira iye mmikono mwanga. Ine ndinati, "M'bale Bosworth, ine ndikufuna ndikufunsemi inu funso. Kodi nthawi yokondwetsetsa yanu inali iti. . .mphindi yanu. . .zaka zanu zonse zimene inu mwalalikira?"

Iye anati, "Pakali pano, M'bale Branham."

Ine ndinati, "Kodi inu mukudziwa kuti mukufa?"

Iye anati, "Ine sindingathe kufa."

Ine ndinati, "Chiyani. . . Inu munganene bwanji kuti ino ndi nthawi yanu yokondwetsetsa?"

224 Panali khomo laling'ono pamenepo. Iye anati, "Ine ndagona pano ndi nkhope yanga italoza ku khomo ilo. Pafupifupi miniti iliyonse, Iye amene ine ndamukonda, ndi Iye amene ndamulalikira ndi kumuimirira, zonse izi. . .moyo wanga, Iye abwera pa khomo limenelo kundidzera ine, ndipo ine ndidzapita ndi Iye." Ine ndinayang'ana pa iye, ine ndinaganiza, ine—ine ndimayang'ana chimodzimidzi mmene ine ndikanachitira kwa Abrahamu, Isaki, kapena Yakobo.

225 Ine ndinamugwira dzanja lake, ine ndinati, "M'bale Bosworth, ife awiri tonse tikukhulupirira Mulungu wofanana, ife timakhulupirira chinthu chofanana. Mwa chisomo cha Mulungu ine ndidzalalikira mpaka mpweya womaliza utachoka mthupi mwanga. Ine ndidzakhala moona kwa Mulungu monga mmene ine ndikudziwira kukhalira. Ine sindidzanyengerera pa Uthenga kumbali iliyonse kapena malo aliwonse. Ine ndidzakhala woona monga mmene ine ndikudziwira kukhalira. M'bale Bosworth, ine ndidzakakumana nanu mu Dziko labwino kumene inu simudzakhala wamng'ono. . .kapena simudzakhala wokalamba nkomwe, koma mnyamata."

226 Iye anati, "Iwe udzakakhala kumeneko, M'bale Branham, iwe usamadandaule."

227 Ndipo ora pambuyo pake, maora awiri iye asanafe. . . pafupifupi miyezi iwiri kenako, ine ndinaganiza iye amafa nthawi imeneyo, mkazi wanga anadzalowa ndipo anamuwona iye (iye nthawizonse ankaganiza zochuluka za mkazi wanga), ndipo kenako Akazi a Bosworth. Ndipo pafupifupi maora awiri iye anali atagona, ali mtulo. Iye anadzuka, iye anayang'ana, ndipo iye analumphu kuchoka pa bedi pake. Iye anati, "Amayi, chabwino, ine sindinakuwoneni inu kwa zaka! Adadi! M'bale Jim, bwanji," anati, "tiyeni tiwone, inu munali mmodzi wa owatembenuza anga kwa Ambuye, ku Joliet, Illinois." Iye anali atafa kwa zaka fifite. Mukuona? Inde! Iye anati, "Ndinu Mlongo *Wakuti-ndi-wakuti*. Inde, ine ndinakutsogolerani inu kwa Ambuye ku—ku msonkhano waku Winnipeg. Eya. Bwanji, apa pali Mlongo *Wakuti-ndi-wakuti*. Ine sindinakuwoneni inu. . .Eya, mwaona, inu munabwera kwa Ambuye *kwakuti-ndi-kwakuti*." Ndipo kwa maora awiri olunjika iye amagwirana

chanza ndi iwo amene iye anawatsogolera kwa Ambuye. Anabwereranso kupita pa malo ake, ndipo anadzagona pansi, anapingasisa manja ake, ndipo zinali zimenezo. Kodi M'bale F. F. Bosworth anakalowa Dziko limenelo limene Yesu anandilola ine kuti ndiliwone usiku wina? Ngati ndi choncho, iye ali kumeneko mnyamata usikuuno. Mulungu apumitse solo yake. Ndipo ine ndikhale wokhulupirika kuti ndidzagalowe Mdziko limenero. Ndipo ine ndikhale a—wantchito woona kwambiri kwa Khristu!

²²⁸ Ine ndikuchita manyazi ndi moyo wanga. Ine ndikuchita manyazi. Ine—ine—ine... Ngati ine ndachimwa pamaso pa anthu inu, inu—inu muli ndi ngongole kwa ine kuti mubwere mudzandiuze ine. Mukuona? Ine ndikuyesetsa kukhala moongoka mu chirichonse chimene Mulungu akundilola ine ndichite mwa chisomo Chake. Mukuona? Mukuona? Koma, onani, amzanga, inu muli ndi ngongole kwa ine ngati inu mukudziwa chirichonse chimene chiri cholakwika ndi moyo wanga, mubwere mudzandiuze ine. Ndipo, onani, ine ndiri ndi ngongole kwa inu kuyima pano ndi kulalikira kwa inu Uthenga woona. Ine ndiri ndi ngongole kwa inu, chifukwa ine ndikuyembekeza kudzawona iliyonse ya nkhope zanu, anyamata ndi akazi, kungowoloka mzere umenewo uko. Iwo ndi mpweya umodzi chabe pakati pa pamene inu muli tsopano ndi kumeneko. Tsopano, uko nkulondola. Ziri kumeneko.

²²⁹ Ndipo Mulungu wachisomo chonse, Mulungu wa Kumwamba, osati mosinjirira, koma molemekeza, “Papa,” pa tsiku lalikulu limenelo pamene ife tizidzaperekedwa kuno ndi kudzakhala ndi matupi athu apa dziko lapansi kenanso, kuti ife tidzakhoze kumwa, ndi kudya mphesa ndi chipatso cha mdzikolo. “Iwo adzamanga manyumba ndipo wina sadzakhalamo. Iwo azabzala minda ya mpesa ndipo wina sadzadya za mmenemo.” Mukuona? Munthu wina kubzala munda wa mpesa, mwana wake nkuwutenga iwo, ndipo kenako mwana wake nkuwutenga iwo, ndi wake. Koma osati mu nkhani iyi; iye adzabzala iwo ndi kumakhala kumeneko. Mwaona, uko nkulondola. Ife tidzakhala kumeneko kwamuyaya. Ndipo mulole, mu Dziko limenelo, ine ndidzakuwone aliyense wa inu.

²³⁰ Ndipo ine ndikudziwa ndikuyankhula muno ngakhale kwa atumiki autatu. Ndipo, abale anga, ine sindikunena izi—ine sindikunena izi kuti ndikupwetekeni. Ndine wautatu, nanenso, ine ndimakhulupirira mu utatu, zikhumbo zitatu za Mulungu (Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera), koma osati Amulungu atatu. Mukuona? Ine ndimakhulupirira kuti ziripo zikhumbo zitatu, mwamtheradi, ine ndimatero ndi mtima wanga wonse, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” koma izo si Amulungu atatu. Izo ndi zitatu zikhu-...kapena za maudio atatu a Mulungu. Mulungu nthawina ina ankakhala mu Utate, Umwana, ndipo

tsopano Mzimu Woyera. Ndi Mulungu yemweyo mu maudindo atatu. Ndipo iwo a . . .

²³¹ Ndipo Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, si Dzina la Mulungu. Mulungu ali ndi Dzina limodzi, ndipo Dzina Lake ndi Yesu. Baibulo linati, “Banja Kumwamba limatchedwa Yesu, ndipo banja pa dziko lapansi limatchedwa Yesu.” Uko nkulondola. Chotero Mulungu anali ndi Dzina limodzi, Dzina la munthu. Iye anali . . . anali ndi dzina lotchedwa Yehova-yire, Yehova-rafa, amenewo anali maudindo Ake a Umulungu. Koma Iye anali ndi Dzina limodzi, Yesu! Ndipo ameneyo ndi Iye.

²³² Ndipo moonadi, abale anga, ngati inu mukutsutsana ndi ine, kumbukirani, ine—ine—ine ndidzakakumana nanu inu kumeneko, mulimonse. Mukuona? Ine—ine ndidzakakhala kumeneko ndi inu. Ndipo Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ine ndimakukondani inu.

²³³ Ndipo ine ndikufuna mpingo kuti ukumbukire tsopano, Lamlungu mmawa ife tidzapitiriza kuyambira apa ndipo ine ndidzayesetsa kuti ndisakusungeni inu motalika kupitirira thuu koloko, kuti ife tidzathe kukhala ndi msonkhano wamasana, ngati ife tingadzakwanitse, ndipo ngati ine ndingachite mwabwino mmene ine ndachitira usikuuno, hafutteni. Inu mundikhulukira ine? Abwenzi, ife sitinatsale ndi nthawi yochuluka, okonedwa. Ine—ine ndakutchulani inu “okonedwa” chifukwa inu muli. Inu—inu ndi okonedwa anga. Inu mukudziwa chiyani? Mundilole . . . Apa pakubwera Lemba. Paulo anati, “Ine ndikukuchitirani inu nsanje (Mpingo Wake) ndi nsanje ya umulungu, pakuti ine ndakupalisani inu.” Ndi zimenezotu, amene amva izo. Ndi zimenezotu. “Pakuti ine ndakupalisani inu, ndakutomeretsani inu kwa Khristu, ngati namwali wangwiro.”

²³⁴ Tsopano, ngati zimenezo zinali zoono pa tsiku limenelo, iye anati . . . Iwo, anthuwo anati kwa ine, anati, “Yesu adzabwera kwa inu, ndipo inu mudzatipereka ife kwa Iye,” namwali wangwiro. “Tidzaweruzidwa ndi Mawu amene inu munalalikira kwa iwo.” Ndipo, taonani, ngati ine ndilalikira kwa inu chimene Paulo analalikira ku mpingo wake, ngati gulu lake lidzakalowe lathu lidzakalowa nalonso, chifukwa ife tiri ndi chinthu chofanana. Amen.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano pamene ife tikuti, “Mulungu akudalitseni inu.” Tsopano . . . ? . . . m’busa wathu wokonedwa, M’bale Neville.



KUKHAZIKITSIDWA ² CHA60-0518
(Adoption ²)

MAULALIKI A KUKHAZIKITSIDWA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu usiku, Mei 18, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org